# *Mlonda, Ndi Nthawi Yanji Ya Usiku?*

[M'bale Gene Goad akuwerenga Yesaya 21:1-12—Mkonzi].

[*Zolemetsa za chipululu cha kunyanja. Monga kamvuluvulu kummwera amadutsa; momwemo iye akuchokera kuchipululu, kuchoka ku dziko lowopsya.*]

[*Masomphenya ovuta anenedwa kwa ine; wamalonda wachinyengo achita chinyengo, ndipo wowononga awononga. Kwera, O Elamu: zungulira, O Mediya; kuwusa kwake konse ndakuletsa.*]

[*Chifukwa chake mchiuno mwanga mwadzaza ndi zowawa: ululu wandigwira, ngati ululu wa mkazi amene akubereka: Ine ndinawerama pansi pakumva izo; Ndinachita mantha powona izo.*]

[*Mtima wanga unalira, mantha anandiwopsyeza ine: usiku wa chisangalalo iye waupanga kukhala mantha kwa ine.*]

[*Konzani gome, yang'anani mu nsanja ya alonda, idyani, imwani: ukani, akalonga inu, ndipo dzozani chishango.*]

[*Pakuti izo Ambuye anena kwa ine, Pita, ukaike mlonda, ulole iye anene chimene achiona.*]

[*Ndipo iye anaona gareta ndi amuna apakavalo awiri, gareta wa abulu, ndi gareta wa ngamila; ndipo anamvetsera mwatcheru ndi kusamala kwambiri:*]

[*Ndipo iye anafuula, Mkango: Mbuye wanga, ine ndiyima mopitirira pa nsanja masana, ndipo ine ndakhala mchipinda changa usiku wonse:*]

[*Ndipo, taonani, apa pakudza gareta la amuna, ndi amuna apakavalo angapo. Ndipo iye anayankha ndipo anati, Babulo wagwa, wagwa; ndipo mafano onse osema a milungu yake aswekera pansi.*]

[*O kupuntha kwanga, ndi chimanga cha pansi panga: chimene ine ndinamva kwa* Ambuye *wa makamu, Mulungu wa Israeli, ndakuuzani inu.*]

[*Cholemetsa cha Duma. Iye akuyitana kwa ine kuchoka ku Seiri, Mlonda, nthawi yanji ya usiku? Mlonda, ndi nthawi yanji ya usiku?*]

[*Mlonda anati, M'bandakucha ukudza, ndipo komanso usiku: ngati inu mufunsa, funsani: bwererani, bwerani.*]

[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

2 Zikomo inu, M'bale Neville. Zabwino kukuonani kenanso.

3 Mmawa wabwino, ku kalasi lathu la Baibulo mmawa uno, pamene ife timakonda kukupatsani inu moni mu Dzina la Ambuye Yesu. Ndipo pamene ine ndimayendetsa mu msewu mphindi pang'ono zapitazo, ndi banja langa, ine ndimaganiza za anthu amene amapita ku tchalitchi mmasiku oterera ngati awa, pamene chipale chiri paliponse mdzikoli, zowopsya pa msewu. Iwo samangobwera kuti adzangowonedwa. Iwo amakhala ndi cholinga chobwerera. Ndipo ndine wokondwa kwambiri kuwona gulu ili pano mmawa uno, kuti, komabe, "Chikhulupiriro cha makolo athu, chikukhalabe," chikuyaka mmitima ya amuna ndi akazi konsekonse.

4 Mawu angowerengedwa kumene ndi M'bale wathu Gene Goad, a mutu wa 21 wa Bukhu la Yesaya, pamene ife tiphunzirepo, kwa kanthawi, ndipo kenako nkukhala ndi pemphero kwa odwala. Ndipo tsopano kwa mutu, mmawa uno, ine ndikufuna kuti nditenge kuchokera pamenepo, ndime ya 11 mpaka ya 12: *Mlonda, Ndi Nthawi Yanji Ya Usiku?*

5 Ndipo ife tisanayambe kuyankhula, tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha mu pemphero.

6 Ambuye Mulungu, Inu ndi Mulungu wa makolo athu. Inu ndi Mulungu Amene munauzira mpweya woyamba wa moyo umene unabwera padziko lapansi, ndipo mwakhala mukulamulira moyo uliwonse mpaka nthawi ino, ndipo mudzalamulira kwanthawizonse. Pakuti Inu ndi Mlengi wa anthu onse, ndi zinthu zonse zimene zimapuma. Inu ndi Mlengi.

7 Ndipo ndife okondwa, mmawa uno, kukhulupirira mmitima yathu kuti malonjezo Anu ndi owona, lirilonse la iwo. Ndi kuti mmalonjezo awa, Inu munanena kuti pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Lanu, kuti Inu mudzakhala pakati pa anthu Anu, ndipo kuti Inu mudzayankha kuitana kwawo.

8 Ndipo pali mitima yolemedwa lero. Kuyambira pamene ndinalowa mu tchalitchi, ndikuwona iwo amene ali pa machira kapena zonyamulira. Ndipo ena mikono yawo ili mmwamba, chifukwa cha matenda—matenda mmikono mwawo. Ndipo ena, ine ndamva, kuti ataya okondedwa awo. Ndipo, oh, ndi dziko lauchimo ndi loyipa! Koma, komabe, zinthu zonsezi zikuyenera kuphunziridwa mwa Ambuye Yesu, Amene anatiuza ife, kuti, "Zinthu zonse zikuchitira ubwino kwa iwo amene amakonda Mulungu."

9 Ndipo ife tikutonthozedwa mmawa uno, kukhulupirira kuti zambiri za zinthu izi zitifikitsa ife pa maondo athu. Ndipo ife timakonda kuganiza za Lemba, kuti, "Iwo amene ayembekezera pa Ambuye adzawonjezera mphamvu zawo. Iwo adzakwera mmwamba ndi mapiko ngati mphungu. Iwo adzathamanga ndipo osatopa. Iwo adzayenda ndipo osakomoka." Ndipo

monga wandakatulo wanena, "Ndiphunzitseni ine, Ambuye. Ndiphunzitseni ine, Ambuye, momwe ndingadikirire."

10 Tiloleni ife, lero, pamene tikuyembekezera kumva kuchokera ku Ulemelero, ndi kuchokera pakamwa pa Mpulumutsi wathu, mwa Mzimu Woyera, kuti ife tidikirira mopirira kuti timve Liwu Lake likuyankhula zinthu zachikondi kwa ife, kudzera mu Mawu Ake, ndi kuyankhula chikhulukukiro cha machimo athu, ndi machiritso a matenda athu.

11 Ndipo mulole ife tichoke pa kachisi uyu mmawa uno, tikusangalala, ndi kunena monga iwo amene anabwera kuchokera ku Emau, "Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu pamene Iye amayankhula kwa ife mnjira?" Pakuti ife tikukhulupirira moona kuti Iye ndi Ambuye wowukitsidwa, monga iwo anamupeza Iye tsiku limenelo. Ndipo Iye ali pakati pa anthu. Sitidzatopa, mitima yathu sidzafooka. Mungotilola ife tiwonjezere chikhulupiriro chathu, ora lirilonse, mwa Inu. Perekani izi, Atate.

12 Ife tikukupemphani Inu kuti mudalitse Mawu olembedwa. Ndi kudalitsa makutu amene ati amvetsere, ndi milomo imene itayankhule; ndipo zitengereni Ulemelero kwa Inunokha. Pakuti mu Dzina la Yesu ife tikupemphera. Ameni.

13 Palibe aliyense wa ife amene ali woti sangakhale ndi mavuto. Mulungu sanalonjeze kuti ife tidzakhala opanda matenda onse. Koma kunalembedwa, kuti, "Mphamvu Zake ndi zokwanira, ndipo Iye sadzaika zochuluka kwambiri pa ife koma zomwe Iye adzatipatse chisomo kuti tipirire." Chotero ife tiri nacho chitonthozo chimenecho chomadziwa.

14 Ku ganizo la mutu pakali pano, kwa mphindi pang'ono, pa chinachake chimene chimawoneka kuti chinayikidwa pa mtima wanga maora angapo apitawa: *Mlonda, Ndi Nthawi Yanji Ya Usiku?*

15 Izo zinali mwinamwake zinali pafupifupi, pakati pa kulowa kwa dzuwa ndi mdima. Ndipo liyenera kuti linali tsiku lowopsya mu mzinda, chifukwa munaperekedwa chenjezo, kuti iwo, mlonda pa nsanja, anali atatumiza uthenga woti anawona chapatali fumbi khobo mmagudumu a magaleta. Ndipo anamva kugunda kwa mapazi a akavalo, pa mtunda wapatali.

16 Koma monga madona aang'ono awiri atayima pachitsime, ndipo mu usinkhu wawo wachichepere, wachinyamata, iwo anali ndi zambiri zoti aziganizire, iwo ankaganiza, kuposa chimene mawu a mlonda ameneyu anali. Mwinamwake izo sizinatanthauze mochuluka kwa iwo, chifukwa iwo anali chabe mu manyazi aukazi wachichepere. Mwinamwake zinali chifukwa chakuti usiku umenewo kunkayenera kukhala phwando, ndipo madona aang'ono awa ankafuna kupita kuphwando limeneli. Ndipo zinkawoneka ngati kuti chenjezo la mlondayo silikanakhala ndi chochita pa chimene iwo

anali nacho chisangalalo chawo cha mdziko usiku umenewo. Chotero pamene kukambirana kumapitirira, ndipo—ndipo dona wamng'ono mmodzi amati kwa mzake, "Kodi izo sizoyipa kwambiri, kuti, mu tsiku lathu, kuti tiri ndi okupha-zisangalalo, wina amene angayesere kuti—kuti atichotse ife pa mwayi umene tiri nawo, ndi zosangalatsa zimene tingamasangalale nazo?"

17 Ndipo ndikukhulupirira kuti izo zingagwirizane ndi mtundu wamakono wa lero, kuti anthu amayesera kuganiza izo pamene ukuyesetsa kukhala tcheru ndi kuwachenjeza iwo za zowopsya zimene zikubwera, kuti iwo amawoneka ngati kuti akuganiza kuti ndiwe chifunga chakale chinachake, winawake amene akuyesetsa kuti achotse chisangalalo chonse mmoyo.

18 Ndipo ife tikhoza kuganizanso za anyamata achichepere, pamene iwo ankachokera ku msonkhano, nkhope zawo zinali zitada chifukwa cha ntchito imene iwo analembedwa masana. Ndipo mnyamata wina akhoza kunena kwa mzake, "Mwamsanga tikangosamba ndi kudzikonzekeretsa, pang'ono, bwanji, tikakumane ku taraveni, monga mwachizolowezi. Pakuti ndikutsimikiza kuti iwe, Yohane, sunasokonezeke ndi uthenga uja umene taumva lero, mlonda uja pa nsanja, akuyesera kuchotsa chisangalalo chonse mmoyo, akuyesera kutiuza ife kuti pali ngozi imene ikuyandikira. Koma, inu mukudziwa, ife tiri ndi ankhondo abwino kwambiri amene alipo. Ndipo ochuluka a asirikali athu ali...timakumana usiku uliwonse pamalo omwewa amene timapitako, ndipo timasangalala ndi chiyanjano pamodzi, monga ngati—kutchova juga kwaubwenzi, ndi zakumwa zina pang'ono. Ndipo ine, pandekha," iye akanati, "ndikukana kuchita mantha ndi chirichonse cha zinthu izi zimene mlonda ameneyu anganene. Pakuti ife tikukhulupirira ngati pakanakhala zowopsya zoti zikubwera, kuti ndithudi athu—aphunzitsi athu akanadziwa za izi, azibusa athu, ndipo bwenzi iwo akutiuza ife za zinthu zoterozo. Ndipo ife sitikusamala kumva nkhani zotopetsa za alonda awa pa nsanja."

19 Ndipo ngati icho sichiri chithunzi chopambana cha fuko lathu lero, kuti achinyamata a mdziko lathu, ndipo osati achinyamata okha, koma achikulire a mdziko lathu, angobalalika. Ndipo iwo akukana kuti amvetsere machenjezo. Ndipo mwamsanga pamene mlonda woona apereka chenjezo, iye amatengedwa ngati wampatuko, kapena wotengeka wina.

20 Ndipo pamene tsiku limapitirira kumalowa usiku, mwinamwake msirikali pa chipata, amene akulondera zipata, amadzakhala wabefu pang'ono. Ndipo iye amapita ku... mlonda wapafupi naye, ndipo amati, "Kodi mukukhulupirira kuti pangakhale mwayi woti mlonda ameneyo akulondola?"

21 Inu mukudziwa, pali chinachake chokhudza chowopsya, pali chinachake chokhudza imfa, chimene chimawoneka

kuti chimakhala ndi kuchenjezeratu kwa izo. Nthawi zambiri okondedwa awo asanawoloke kupita ku tsidya lina, zikumawoneka kuti pamakhala chenjezo limene limabwera kwa iwo.

22 Ine ndikukhoza kuganizira za abambo anga, iwo asanachoke. Iwo anali atachoka ku Kentucky kwa zaka zambiri. Koma, mwadzidzidzi, chinachake chinkawoneka kuti chimawasuntha adadi, kuti apite kumusi kumalo a nyumba yakale ndi kukayankhula ndi okondedwa awo ndi azimzawo.

23 Atabwerera kunyumba, mchimwene wawo, amene sanathe kumuwona, anachenjezedwa mwachirendo kuti abwere ku Jeffersonville kudzawawona iwo. Ndipo pamene iwo anali atakhala, akuyankhulana, adadi anawolokera kupita ku dziko linalo.

24 Ine ndikuganiza za apongozi anga aamuna. Patangotsala masiku pang'ono kuti azichoka, iwo anati, "Billy, tiye iwe ndi ine tipite tikasake agologolo, pamwamba pa Utica. Ndikungofuna kuti ndipite kumalo akalewo." Mwanjira ina, mchigawo cha Mulungu, ine sindinathe kupita nawo tsiku limenero. Ndipo iwo anapita tsiku limenero ndipo anakasaka, ndipo pamene anabwerera kumusi mu basi, iwo—iwo anandiuza ine, iwo anati, "Ine ndinali nditakhala pamwamba pa phiri. Zonse zinasintha tsopano. Koma pansi penipeni pa ngodya ina ya nkhalango, ku Battle Creek, basi pamwamba pathu," iwo anati, "zimawoneka ngati ndimawamva amayi anga akuyitana, 'Oh, Frankie!'" Usiku umenewo iwo anapereka umboni, mu mzere wachiwiri wa tchalitchi chino, kumanzere kwanga, akukhumba mapemphero a anthu a iwo. Ndipo patadutsa masiku angapo, ife tinakawayika iwo mmanda.

25 Izo zimangowoneka kuti Mulungu nthawizonse amatumiza mtumiki. Ndi ubwino Wake ndi chisomo Chake, kuti aziwapatsa owona mu mtima chenjezo la zinthu zimene ziri nkudza.

26 Ndipo ndine wokondwa kwambiri kuti mu tsiku ili limene ife tikukhalamo tsopano, kuti, pamene kulunda ndi mdima ziri pa mbali iliyonse, pakuwoneka kuti pali chiyembekezo chodala chagwira mitima ya anthu a Mulungu, kuti ora lina laulemelero Yesu afika.

27 Ndipo mu nthawi yaikulu iyi yamavuto, mu mzinda uwu, achichepere akunyalanyaza izo, ndi anthu ambiri amene sanalabadire chimene mlonda amanena. Ndithudi, iwo anali mu bala, akumwa, ndipo phwando linali likupitirira. Ndipo asirikali onse anali akumwa. Ndipo amakhala ndi nthawi yopambana, amaganiza kuti iwo anali otetezeka basi momwe iwo akanakhalira. "Palibe chimene chikanawavulaza iwo," chifukwa iwo anali atangoyatsidwa mophweka, monga ife tingazitchulire izo, pa mizimu ya kachasu ndi zakumwa zosakaniza.

28 Ndipo mwadzidzidzi, panadzabwera magareta akugudubuzika akulowa mu mzinda. Ndipo zitseko zamu bala zinathyoledwa, ndi nyumba, ndipo zida zophera zinali zikugwira ntchito, basi chifukwa chakuti iwo anakana kumva chenjezo la mlonda.

29 Ndipo ntchito za mlonda, mu Baibulo lakale, anali munthu amene amasankhidwa. Iye amayenera kukhala munthu amene amakhala watcheru ndi zinthu za zammwamba. Iye amayenera kumadziwa ndendende basi pamene nyenyezi zikupachikika, kuti anene nthawi yeniyeni kwa anthu. Ambiri otopa, amatuluka, mwinamwake, ndipo amalephera kuti agone, abefu, ndipo amafuulira pa mlonda mu nsanja, ndipo amakhoza kufuula mokweza mawu awa, "Mlonda, ndi nthawi yanji ya usiku?"

30 Ndipo ankayang'ana nyenyezi, ndipo kenako amati, "Ndi nthawi *yakuti-ndi-yakuti*."

31 Kenako iwo amabwerera pa bedi pawo, kapena kulikonse kumene iwo amasankha kukakhala, akudikirira kuti kuwala kwa tsiku kubwere, pamene usiku wotopetsa, wofooketsa, wosowetsa mtendere udzathe.

32 Mulungu tichitireni chifundo! Ine ndikudabwa ngati iyo si nthawiyo, lero, imene ife sitinayitanire kwa Mlonda wathu wamkulu, "Ndi nthawi yanji ya usiku?" Pali ngozi imene ikubwera, ndipo dziko lonse likuwoneka kuti likugwedezeka chifukwa cha chikoka chake.

33 Mlonda nayenso ankayenera kukhala pa ntchito, nthawi zonse. Ndipo iye ankayenera kuti aziwachenjeza anthu za zowopsya zimene zikubwera. Imeneyo inali ntchito yake, kuyang'anira ngozi imene ikubwera. Ndipo iye anali pamwamba pa nsanja imene inamangidwa motalika kwambiri kuposa zipupa. Ndipo nsanja iyi, iye anali nawo kumtunda uko, mmenemo, mabukhu a ukasidi, ndi zina zotero, kuti azitha kuyang'ana nyenyezi ndi kudziwa nthawi. Chinthu chirichonse choyandikira, cha nthawi ya tsiku, iye amakhoza kuchinena icho.

34 Kenako, iye amathanso kuwona patali kwambiri kuposa aliyense amene anali pansi. Iye ankatha kuwona patali kuposa aliyense amene anali pa mpanda, chifukwa iye amakhala pamwamba kwambiri. Ndipo pamene ukukwera mmwamba, ndi pamene umawona patali. Ndipo ukhoza kudziwa zowopsya zimene zikubwera, kutali kwambiri kuposa amene ali omangika pa dziko.

35 Ndipo monga Yesaya, mu tsiku lake, ankayankhula kuti Mulungu anamupanga iye kukhala mlonda. Mulungu amafanizira aneneri Ake ngati mphungu.

36 Ndipo monga ndimalalikira kawirikawiri za phunziro la mphungu, mphungu ndi mbalame imene imatha kupita

mmwamba kuposa mbalame ina iliyonse. Ndipo iyo imayenera kupangidwa mwapadera chifukwa cha utali umene iyo imapita. Tsopano, khwangwala sangathe kuitsatira iyo. Palibe mbalame ina imene ingatsatire iyo. Iyo ndi mbalame yopangidwa ndi Mulungu, ndipo inapangidwa chomwecho. Ngati mbalame ina iyesera kutenga malo ake, iyo ingakawonongekeko. Iye amayenera kukhala ndi nthenga zolimba, mapiko amphamvu. Ndipo zingamuchitire ubwino wanji kukwera mmwamba ngati sakutha kupenya, alibe maso abwino kuti azipenyera? Khwangwala akhoza kukachita khungu mmwamba kumeneko; iye sangathe kuwona. Koma mphungu ikamakwera mmwamba, ndi pamene iyo imawona patali.

37 Ndipo Mulungu amawafanizitsa aneneri Ake ndi mphungu. Iwo ndi azilonda amene amakwera pamwamba, kuti aziwona patali. Ndipo maso awo anapangidwa kukhala auzimu kuti azitha kuwona zowopsya zimene zikubwera.

38 Ndipo Mulungu anali atamuika Yesaya pamwamba kuti awachenjeze anthu kuti kukubwera chowopsya, ndipo iwo sanamumvere iye.

39 Ndipo, lero, Mulungu akadali nazobe mphungu, kapena amithenga, kapena anthu pa nsanja, amene amakwera mu Mzimu, kutali kudutsa machitidwe onse, ndi mabomba onse a atomiki, ndi kafukufuku wasayansi. Iye ali nawo amuna amene anapangidwa mwapadera kamba ka cholinga chimenecho, amene amakwera pamwamba pa makoma a Kalvare, mu Dzina la Ambuye Yesu, ndipo amayima pamwamba pa mtanda, ndipo akhoza kutumizanso Uthengawo, "PAKUTI ATERO AMBUYE." Kupenya kwawo kwauzimu ndi kwakukulu kwambiri kuposa ansembe mu kachisi; kutali kuposa munthu wamba wa kuyenda kwa moyo; pakuti iwo anapangidwa mwapadera kuti azigwira ntchito zimene Mulungu wawayitanira iwo. Choncho, zimatipindulira ife tikamvera pamene timva zinthu zimene ziri nkudza.

40 Ndiye ine ndingasinthe tsopano kwa mphindi chabe. Ndipo ndingatembenuzire tcheru chanu kwa Mfumu ya mphungu izi, kapena aneneri, kapena alonda apa nsanja. Ameneyo ndi Ambuye Yesu, Iyemwini. Ndipo tsiku ili limene ife tikukhalamo linali lalikulu kwambiri kuposa tsiku limene Iye anali kuno, mpaka, pamene Iye anali mu mithunzi ya mtanda, Iye anayankhula mochuluka za Kudza Kwake kwachiwiri kuposa momwe Iye anachitira za kuchoka Kwake. Ngati mungafufuze Malemba mosamala, mupeza kuti basi Iye asanachoke, kuti Iye ananenera za zinthu zimene zikanati zidzachitike mu tsiku lino.

41 Iye ankadziwa kuti Iye amayenera kupachikidwa. Iye ankadziwa kuti Iye amayenera kuvutika a—wosalakwa chifukwa cha wolakwa. Iye ankadziwa kuti Iye adzauka kenanso kuchokera mmanda, pa tsiku lachitatu. Iye ankadziwa

kuti panalibe mphamvu zimene zikanamugwira Iye mmanda, chifukwa Mawu a Mulungu anali atanena, "Ine sindidzalola woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi, komanso Ine sindidzasiya moyo Wake mu gehena." Ndipo panalibe mphamvu zimene zikanaphwanya ulosi umenewo. Mawu Ake adzakhala owona, ndipo Iwo adzakwaniritsidwa mu nyengo Zawo. Ndipo Iye anali ndi chidaliro kuti, chimene Atate anali atanena, Atate anali wokhoza kusunga Mawu Ake.

42 Chotero, mtima Wake waukulu umene unali mwa Iye, umene unali Mpandowachifumu wa Mulungu, mu mtima Mwake Iye ankadziwa kuti nthawi zoyesa zazikuluzi izi zidzabwera kudzatsimikizira mafuko onse, ndi kudzawatsimikizira anthu onse. Chotero, choncho, Iye ankadziwa kuti funso lalikulu linagona, osati ngati Iye adzaukanso, kapena ngati Iye akanadzapachikidwa monga mwa Malemba, kapena osati ngati Iye akanakwera Mmwamba, ndipo Mzimu Woyera ukanadzabwera. Koma funso linali lakuti, "Kodi pakanadzakhala chikhulupiriro chirichonse chotsalira pa dziko pa Kudza Kwake?" Ndipo kodi chikhulupiriro chimachokera kuti? "Pakumva Mawu a Mulungu." Limenero linali funso Lake. "Kodi padzakhala chikhulupiriro padziko lapansi pamene Ine ndidzabwera?" Kodi Iye adzawapeza anthu amene amakhulupirira Mawu Ake?

43 Tsopano pamene ife, mu tsiku limene ife tikukhalamo, tikhoza kutembenukira ku masamba a Mawu Ake odala, ndi kudzapeza zinthu zomwezo zimene Iye ananena kuti zikanadzachitika, zikuyandikira pa dziko lero, zizindikiro ndi zodabwitsa zikuchitika: "Mitima ya anthu ikulephera ndi mantha." Pali "kusokonezeka kwa nthawi ndi kupsyinjika pakati pa mafuko. Mawonekedwe owopsya mu mlengalenga," monga zimbale zowuluka, ndipo Pentagon yonse yagwedezeka. "Ndipo nyanja ikubangula, ndi zivomezi mmalo osiyanasiyana. Mitima ya amuna ikulephera, mwa mantha." Zida zazikulu za atomiki zakonzeka, zikudikirira. Mdima wapachikika pa dziko lapansi, umene dziko lapansi silinawuwonepo.

44 Sabata yatha ndinali ndi mwayi woyankhula ndi mmodzi wa azimzanga okondedwa ndi abale, Captain Julius Stadsklev, amene analemba bukhu, *Mneneri Achezera Afrika*. Ndipo M'bale Julius anali mu California, kumene iye tsopano akutenga maphunziro ake a utsogoleri mu usirikali. Ndipo iye... Iwo, anthu aku usirikali, anamutengera iye ku mayesero aakulu. Ndipo iwo anafufuza mibadwo ya makolo ake mpaka anatsimikizira kuti agogo a agogo ake anali ndani, ndi mbiriyakale yawo ndi chimene iwo anali, iye asanakhale mu msonkhano uwu.

45 Ndipo pamene iye ankabwera kuchokera ku msonkhano, ndipo anafika pamwamba pa phiri pamene ife tinkakhala ndi abwenzi ena, iye anakomana nane kunja uko pansi pa mtengo

wa tsanya, ndipo iye anati, “M’bale Branham, ndi chinthu chotopetsa kwambiri chimene inu munayamba mwachimvapo.” Iye anati, “Ndiri pansi pa kulumbira kwakukulu kumene sindingathe kunena, kapena sindingathe kutulutsa nkhani iliyonse,” anati, “chifukwa ndife. . .Iwo anatitengera ife kukalumbira mwaulemu. Koma,” anati, “Ndikhoza kunena ichi. Gulu la nkhondo akulithetsa. Iwo sakhalanso ndi gulu la nkhondo linanso; angokhala ndi azilonda pang’ono okha. Sakhalanso ndi ndege zina zowonjezera. Iwo satero ayi—sayika nthawi yawo popanga ndege zaliwiro ndi zina zotero, pokhapokha ngati ili ya malonda. Iwo akukhala akuyesetsa zokhethemula kamodzi mfuti. Akatero padzabwera chiwonongeko chathunthu.”

46 Iye anati, “M’bale Branham, anthu sakudziwa chimene zinsinsi za zinthu zankhondo ziri.” Iye anati, “Pamene ma ofesala aakulu awa amayankhula mchipindamo,” iye anati, “apo panadza mdima wowopsya chomwecho mchipindamo, mpaka mmodzi wa asayansi awo wamkulu anaimirira, ndipo anati, ‘Ndikanakonda ndikanatenga ngolo yakale ndi ng’ombe, ndi kubwerera kuseri kwa mapiri, ndi kukabzala kandime ka kabichi ndi nyemba, ndi kuiwala zonse za izo.’ Oh,” iye anati, “izo zingati, ngati nkhani iyi ingakafike ku gulu kwa anthu, dziko lonse lingapanikizike. Chowopsya chikuyandikira.”

47 Iye anati, “Iwo ali. . .akuwachotsako antchito awo tsopano kuchokera ku zilumba. Iwo akuchotsako magulu awo kuchokera ku England. Ndipo iwo ali ndi ngalawa zazikulu ziri kunja uko, ndi mtundu wina wa zida. Ndipo iwo akungoyembekezera kamvuluvulu woyamba wa bomba, ndipo fuko lirilonse lidzamasulidwa nthawi yomweyo.” Anati, “Sipadzakhala mphukira imodzi ya udzu yotsalira padziko lapansi, kapena phiri limodzi koma zimene zidzagwedezeke mpaka kufika pa msinkhu wake. Ndipo izo zikhoza kuchitika nthawi iliyonse.” Oh, ora lolunda bwanji!

48 Ndipo zinthu zonsezi zimene mumazimva za mbale zowuluka. Ndipo inu munamva zokambirana ndi mwamuna ameneyo, ine ndikuganiza, dzulo, pa wailesi, amene amadzinenera kuti iye anayankhula ndi anthu. Ine sindikufuna kumunyozetsa mwamuna ameneyo, koma kachitidwe kake konse ndi kosiyana ndi Mawu. Iko sikolondola. “Ndipo pa Mars, iwo alibeko imfa, ndipo iwo abwera kuno kudzatiphunzitsa ife momwe tingakhalire opanda imfa.” Koma pamene zinafika potsimikizira, iye analibe kachidutswa kamodzi ka umboni, kuti akhoze kutsimikizira izo. Basi lingaliro lina lanthano chabe limene iye analipanga. Ndipo, mwa kuganiza kwanga, ndi zabodza, chifukwa Baibulo linanena mosiyana ndi zimene iye ananena.

49 Ine ndikhoza kufotokoza zomwe ndikuganiza za mbale zowuluka. Ine sindikukhulupirira kuti izo ndi mithunzi. Ine

sindikukhulupirira kuti ndi nthano. Ine ndikukhulupirira . . . Ndipo izi sizikupanga izo kukhala zolondola. Ndi lingaliro langa chabe. Ambuye sanandiuze kuti ichi ndi chimene izo ziri. Koma, poyang'ana mu Malemba, pakuti Mmenemo ndi momwe timapezamo zinthu zonse.

50 Yesu anati, "Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu." Ndipo chisanachitike chiwonongeko cha Sodomu, ndipo moto unagwa ndi kuwotcha mzindawo ndi zigwa, panali Angelo amene anatumizidwa kuchokera Kumwamba, amene anayang'ana ndi kudzafufuza, kuti apeze ngati zinthu izi zinali zoona kapena ayi. Ndipo kodi izo sizingakhale ngati Mulungu akutumiza Angelo Ake kuti adzafufuze ndi kudzapeza, basi chiwonongeko chachikulu chisanafike? Ndipo kodi inu munazindikira? Panali Mngelo mmodzi Amene anabwera, Amene anadzachezera munthu wokalamba amene anali atapanga chisankho chomusankha Mulungu, ndipo ankakhala, akunyozedwa ndi dziko, mu hema ku chipululu uko, chifukwa winawake anali atasankha ndipo anatenga chuma chake chonse. Koma iye anati, "Izo zonse nzabwino. Ine ndingokhala pano mu chifuniro cha Mulungu."

51 Ine kulibwino ndikhale mu chifuniro cha Mulungu kuposa kukhala ndi ndalama zonse zimene dziko lingakhoze kukupatsa iwe.

52 Ndipo mwamsanga pamene lingaliro lotsiriza limenero linapangidwa, kenako Mngelo wa Ambuye anadza kwa Abrahamu ndipo anati, "Yang'ana kummawa, kumadzulo, kumpoto, ndi kummwera. Zonsezo ndi zako, Abrahamu."

53 Malemba amatiuza ife, "Odala ali ofatsa: chifukwa iwo adzalandira dziko lapansi." Kodi izo zimapanga kusiyana kotani? Zinthu zonse za mdziko lapansi zidzatha limodzi ndi dziko lapansi, koma Mulungu sangawonongeke konse.

54 Ndipo ine ndimakhulupirira monga, ndimatsogozedwa kukhulupirira, ndiko kuti, ngati chithunzi cha Mngelo wa Ambuye Amene amabwera ndi kudzachita zozindikira . . .

55 Kodi inu munazindikira Mngelo Amene anabwera kwa Abrahamu? Iye anali atatembenuzira nsana Wake ku hema, pamene Iye ankayankhula ndi Abrahamu, ndipo anati, "Ine ndisunga lonjezo Langa kwa iwe."

56 Oh, ndi Uthenga bwanji wa Mngelo wa Mulungu mu tsiku lino, Amene ati adzasunge lonjezo Lake! Kusakhulupirira konse kwa mdziko, okaikira, otsutsa zaumulungu, ndi achikunja, ndi osakhulupirira, sadzapangitsa Mphamvu ya Mulungu kukhala yopanda chochita. Izo zidzachitika chimodzimodzi basi.

57 "Ndidzakumbukira lonjezo Langa, ndipo ndidzapanga lonjezo Langa kukhala labwino." Ndipo Sarah anaseka mu hema kumbuyo Kwake.

58 Ndipo atatembenuzira nsana Wake ku hema, Iye anati, "Nchifukwa chiyani Sarah anaseka?"

59 Ndipo Sarah anathamanga ndipo anati, "Ine sindinaseke," chifukwa ankachita mantha.

60 Kodi uyu anali Munthu wa mtundu wanji? Ndikudabwa kuti anali Mlonda wotani pa nsanja pamenepo? "Ndi umunthu wa mtundu wanji uwu umene uli ndi ife, atatembenuzira nsana Wake kwa ine, komabe akudziwa kuti ine ndinaseka, mu hema?" Kumbukirani, Iye anali Mlonda.

61 Ndipo Iye anatembenuka, ndipo Iye anati, "Inde, iwe unaseka." Ndipo iye anachita mantha.

62 Tsopano, ife tikuzindikira kenanso, kuti mu tsiku lino Kudza kwa Ambuye kusanafike, Anthu omwewa akuyenera kubwereranso kachiwiri. Ndipo ine ndikudabwa, pamene ife tikuyang'ana mozungulira ndi kuwona chikhalidwe cha Iwo, penyani zimene Iwo akuchita, ndipo ndikudabwa ngati zambiri mwazinthu zodabwitsa izi siziri ndendende zomwe Yesu ananena kuti zidzachitika. "Padzakhala zizindikiro mmiyamba kumwamba. Ndipo pa dziko lapansi padzakhala kupsyinjika pakati pa mafuko, kusokonezeka kwa nthawi, zivomezi mmalo osiyanasiyana, ndipo amuna akufa ndi kulephera kwa mtima." Osati akazi; amuna. Akazi samafa kawirikawiri ndi vuto la mtima. Ndi amuna. Izo zikukwaniritsa zimene Yesu ananena kuti zidzakhala. Ndizo ndendende zimene Iye ananena kuti zikanadzakhala.

63 Ndiyeno monga ife tingakhoze kumapitirira, ora ndi ora, pa aneneri onse, momwe iwo ananenera za tsiku lino. Kodi izo sizingapangitse wina kufuula, "Mlonda, ndi nthawi yanji ya usiku?"

64 Pentagon ilibe yankho. United States ilibe yankho. Germany, Russia, palibe aliyense wa iwo amene ali ndi yankho. Sayansi ilibe yankho.

65 Ndani ali ndi yankho? Mlonda, amene ali pa mpanda, ali ndi yankho. "Mlonda, ndi nthawi yanji ya usiku?" Ndipo Mzimu Woyera ndi Mlonda amene akukonzekeretsa anthu, ndi kupereka machenjezo ochokera kwa Mulungu. Waikidwa kukhala Mlonda. Ife tikuwona odwala akuchiritsidwa, maso akhungu akutseguka, makutu ogontha akutsegulidwa, olumala akuyenda, olumala akuwukha . . . akutsimphina ngati nswala. Kukwaniritsa a . . . Icho ndi chiyani? Ndi Kudza kwa Ambuye, kukukangamirabe.

66 Ndi zinthu zonsezi, ndi machenjezo awa! Ndipo anthu kumapitirirabe kulimbanirana kupita ku maphwando awo a mowa, mpaka nthawi zawo zopusa. Ndipo akumachita masewero. "Ndipo akumavina, ndipo akumadya, ndipo akumamwa, ndipo akumakwatira, ndipo akuperekedwa mchikwati," basi monga Mulungu ananenera kuti zidzachitika. Palibe njira yowaletsera iwo.

67 Ndiye ngati inu mungazindikire, mu m'badwo wa mpingo waukulu uwu, molingana ndi Chivumbulutso 3, pa m'badwo uwu tsopano anali amene anapatsidwa Nyenyezi ya Mmawa, basi Kudza kusanachitike.

68 Yang'anani momwe Yesaya analiri Mwamalemba pamene iye anati, "Mlonda, ndi nthawi yanji ya usiku?" Iye anati, "Mmawa wafika, ndipo usikunso." Chiyani? Mmawa wafika, koma usiku umafika kusanache. Icho chinali chiyani? Aliyense akudziwa kuti tsiku lisanache, basi pa maora oyandikira tsikulo, kumadzakhala mdima woposa umene unalipo.

69 Oh, abwenzi anga, mvetserani kwa PAKUTI ATERO AMBUYE. Ngati mumanditenga ine kuti ndine wantchito Wake, kwangotsala pang'ono kuti kuche. Ndi chifukwa chake kulunda kowopsya uku kuli padziko lapansi. Izo ziri Kudza kwa Ambuye Yesu kusanachitike. Palibenso chiyembekezo chatsalira mu chirichonse koma Kudza Kwake.

70 Mafuko akutsutsana ndi mafuko. Ndipo iwo achita zopusa mu laboratare ya Mulungu mpaka iwo ali ndi mphamvu yophulitsana wina ndi mzake kukhala phulusa la atomiki. Ndipo iwo ndi oyipa, ndipo iwo si achipembedzo, ndipo iwo ndi osakhala-ngati-Khristu. Ndipo chokhumba chokha chimene ali nacho, ndi cholinga, ndi kuwononga. Ndipo iwo adzodzedwa ndi mngelo wowononga amene anatumizidwa kuchokera kumwamba kudzawadzoza amuna amenewa.

71 Mundirole ine ndinene, mu Dzina la Ambuye Yesu, Mzimu Woyera watumizidwa ngati Mlonda pa nsanja. Ndipo pamene anthu akufuula, "Ndi nthawi yanji ya usiku?" Kodi mwatopa ndi moyo uno? Kodi mwatopa ndi tchimo? Kodi mwatopa ndi miyambo ya maliro, ndi matenda, ndi kupanda umulungu kumbali zonse? Kodi usiku wakhala wautali komanso wotopetsa? "Ndi nthawi yanji ya usiku, Mlonda?"

Iye anati, "Mmawa ukubwera." Mukuona chitonthozocho?

72 "Ndipo usiku nawonso ukubwera." Usiku ndi chiyani? Taonani momwe mu mgwirizano wangwiro ndi Lemba, Yesaya anali. Mu kachitidwe ka chizolowezi ka—ka chirengedwe, nthawizonse kumakhala kuyandikira kwa dzuwa kumakokera mdima pamodzi ndi kuchititsa iko mdima. Kumakhala mdima kusanache kuposa nthawi ina iliyonse usiku. Chifukwa chiyani? Ndi kuwala kumene kukubwera kumene kukupangitsa kuti pakhale mdima.

73 Ndipo ndi kuyandikira kwa Ambuye Yesu tsopano kumene kukubweretsa mdima uwu pa dziko lapansi. Kodi Iye sanati, "Pamene zinthu izi zidzayamba kuchitika, mudzakweze mutu wanu, pakuti chiwombolo chanu chayandikira"?

74 Palestina ndi fuko. Ayuda abwerera kuchokera ku dziko lonse lapansi, ndipo akaikidwa uko kuti amuwone Iye akamabwera, monga Mulungu ananenera kuti iwo

akanadzatero. “Phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu, pamene iwo uyamba kutulutsa mphukira zake.” Iye anati, “Momwemo kudzakhala kuti m’badwo uwu sudzatha, sudzathedwa, iwo sudzatha, mpaka zinthu zonsezi zidzachitidwe.” M’badwo wanji? M’badwo umene udzawone mkuyu ukuphuka masamba ake. Israeli nthawizonse wakhala ali mtengo wa mkuyu.

75 “Chimene chimbalanga chinasiya, anoni anachidya,” anatero Yoweli. “Chimene anoni anasiya, chirimamine anadya. Ndipo chimene chirimamine anasiya, dzombe linadya.” Ndipo ngati mungazindikire, iko ndi kachirombo komweko. Chirichonse cha tizirombo ito timene timadya mtengowo, ndi kachirombo komweko, kokha pa usinkhu wosiyana. Ndipo tchimo lomwelo ndi kusakhulupirira zimene zinayamba kuwadya Ayuda, kuti, “Yesu sanali Khristu,” zimene zimadya mtengowo kukhala chitsa chosabala. Ndipo mneneriyo anawona izo, ndipo analira. Koma Ambuye anati, “‘Ine ndidzabwezeretsa,’ atero Yehova, ‘zaka zonse zimene anoni, ndi dzombe, ndi chimbalanga zinadya.’”

76 Ndipo kwa nthawi yoyamba kwa zaka twente-faivi handirede, Ayuda akubwerera ku dziko lawo. “M’badwo umenewo sudzathetsedwa, sudzachoka, mpaka zinthu zonsezi zitakwaniritsidwa.” “‘Zikadzatero Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga mmasiku otsiriza,’ atero Mulungu, ‘pa ana Anga aamuna ndi aakazi, ndipo iwo adzanenera. Ndipo ndidzawonetsera zodabwitsa.’”

77 Odwala akuchiritsidwa, mphamvu zazikulu zikuchitika, mwa Mzimu womwewo umene unakhala ndipo umatha kumuuza Abrahamu kuti Sarah anaseka mu chipinda kumbuyo kwa Iye.

Kenako ife timafuula, “Mlonda, ndi nthawi yanji ya usiku?”

78 Ndipo iye anati, “Usiku ukudza.” Penyani. Usiku, choyamba . . . Mmawa ukudza, choyamba. Kenako, usiku, nawonso.

79 Kukangotsala pang’ono kucha, nthawizonse pamakhala kuwala kumodzi kwakukulu kumene nthawizonse kumaikidwa mmiyamba, ndipo iyo ndi nyenyezi ya mmawa. Pamene muwona nyenyezi ya mmawa ikuwala, kuwala ndi kuwala, ndiye dziko limakhala likuchita mdima ndi mdima. Ndipo chifukwa chimene iyo ili yowala kwambiri, ndi chifukwa dziko lapansi ndi la mdima kwambiri.

80 Ndipo Mpingo wa masiku otsiriza ano, oyitanidwa atuluke ndi Thupi losankhidwa la Khristu, analonjezedwa ndi Baibulo kuti Iye adzawapatsa iwo Nyenyezi ya Mmawa.

“Mlonda, ndi nthawi yanji ya usiku? Kodi chitachitike ndi chiyani?”

81 Ndi ichi apa. Chiwonongeko chathunthu chikubwera padziko lonse. Koma chiwonongekocho chisanachitike, Mpingo

wa Yesu Khristu udzapita mu Mkwatulo, kukakomana ndi Ambuye Wake.

82 Kodi nyenyezi yammawa ndi yoti idzachite chiyani? Kodi ndi chiyani chimapangitsa nyenyezi kukhala zowala kwambiri panthawiyo? Ndi kuyandikira kwa dzuwa. Nyenyezi yammawa ikunyezimiritsa kuwala kwa dzuwa. Nyenyezi zina zimawoneka kuti zikuzima pa ora limenero.

83 Zaumulungu zonse zopangidwa ndi anthu, kuzizira konse, kusayanjanitsika kwa mwambo kudzauma. Koma mlonda uja atakhala kutsidya pa nsanja, ndi Nyenyezi ya Mmawa, adzanyezimiritsa Uthenga woona wa Ambuye Yesu umene uyandikire posakhalitsa, chifukwa Iye akuwala ndi kuwala, nthawi zonse, pamene dzuwa likuyamba kutuluka.

84 Oh, ine ndinganene kuti, nyenyezi zammawa, ukani ndipo muwale kwa ulemelero wa Mulungu, pakuti kuyandikira kwa mdima wapakati pa usiku kuli pa dziko lapansi, ndipo mdima wokhudzika uli pa anthu. Koma mmawa ukudza, ndipo nyenyezi zikuyenera kumapereka kuwala kwake.

85 Taganizani za ora loyipa limenelo limene likuyang'anizana ndi dziko lonse. Taganizani za mdima wowopsya umenewo umene ukuyang'anizana ndi munthu aliyense wosapulumutsidwa lero. Mafuko onse, ndi mapiri onse, ndi minda yonse ndi nyumba zonse zimene iwo ankakhala nazo ulemelero, zidzasanduka ufa, ku maphulusa a chiphala chamoto kenanso, mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso.

86 Koma iwo amene amakonda Ambuye, iwo amene ali ndi Kuwala kwa Nyenyezi Yammawa, amene akufika—amayika maso awo pa Iye, ndi kuchoka ku zinthu za mdziko! Ndipo monga Paulo analembera mu kalata yake yotsekera, iye asanachoke pa dziko lapansi, iye anali wofooka, ndi wamanjenje, ndi wotopa. Oh, momwe ine ndikumverera za Myuda wamng'ono ameneyo. Pamene iye anati, "Musalole aliyense andivutitse ine. Ndamenya nkhondo yabwino, ndipo ndatsiriza ntchito yanga. Ndasunga chikhulupiriro. Ndipo kuyambira pano pali korona wa chirungamo amene Ambuye Woweruza wolungama adzandipatsa ine pa tsiku limenero." Kenako iye anaganiza za kudza kwa nyenyezi za mmawa, ndipo anati, "Osati kwa ine ndekha, koma kwa onse amene amakonda kuwonekera Kwake." Oh, "Dzutsani mitu yanu, chiwombolo chanu chayandikira."

87 "Mlonda, ndi chiyani chikupangitsa pepala kunena izi? Nchiyani chikupangitsa sayansi kuwopa kusuntha? Nchiyani chikupangitsa Pentagon kuchita mantha kutulutsa nkhaniyo?" Chifukwa anthu akhoza kudzipha ndi kutaya ndalama zawo mmisewu, ndi zinthu. "Kodi akanatani . . . Vuto ndi chiyani? Icho ndi chiyani? Ndi nthawi yanji ya usiku?"

88 "Mmawa ukubwera." Uko nkulondola. Kodi zonsezi ndi za chiyani? Ndi kupangika kwa mmawa, kukubwera,

ndipo kukukankhira patsogolo Kuwala. Zikupanga mdima wokhudzika kubwera Kuwala kusanayambe kuwala.

89 Ndine wokondwa kwambiri kukhala Mkhristu. Ndine wokondwa kwambiri kuti ndine mlonda Wake, mmodzi wa iwo, amene wayima pa mpanda, akufuula, "Konzekerani kukumana ndi Mulungu, pakuti ora la Kudza Kwake likuyandikira."

90 Ndipo inu, muno mu tchalitchi chino mmawa uno, ngati pali mmodzi amene sali wotsimikiza kuti Nyenyezi ya Mmawa ikunyezimiritsa Kuwala Kwake mu mtima mwanu, Mzimu Woyera waukulu, mukhale mukukonzekera zimenezo. Pakuti pali chochitika chimodzi chachikulu kwambiri chimene chinayamba chachitikapo, chiri pafupi pakali pano. Ife tayima mmphepete, tikuwonerera sewero likuyambika.

91 Ine nthawi zambiri ndawonerapo makanema, momwe ku Hollywood ndi malo osiyanasiyana, amapangira masewero awo. Ndi momwe iwo amatengera akatswiri awo, ndi awo ena otero, ndi kuwakonza iwo. Ndi momwe amawaphunzitsira iwo ndi chirichonse sewero lalikulu lisanayambe. Ine nthawizonse ndimakhala wodabwitsidwa ndikamawonera izo, ndipo ndinkadziwa kuti izo zimayenera kukhalapo zabodza.

92 Zinthu zonse zabodza zimapangidwa kuchokera ku zenizeni. Sipangakhale dola yabodza mpaka patakhala yeniyeni. Sipangakhale wachinyengo pokhapokha patakhala Mkhristu weniweni. Sipangakhale uthenga wabodza pokhapokha patakhala Umodzi woona. Sipangakhale usiku pokhapokha patakhala usana. Ndithudi!

93 Ndipo pamene ndimawawona iwo akukonzekera masewero awo, ndipo ine ndimaganiza, "Oh, ife taima patali pa nsanja, pamwamba pa chirichonse mdziko lino, ndipo ife tikuyang'ana zinthu ziwiri zazikulu; kutha kwa nthawi, ndi Kudza kwa Ambuye." Posachedwapa, "Nthawi sidzakhalaponso." "Sipadzakhalanso nthawi," ndi Kudza kwa Ambuye.

94 Ndipo wotsutsakhristu, ali ndi omutsatira ake akhala pamenepo. Iye ali ndi chikominisi. Iye ali ndi timalingaliro tosiyanasiyana: iye ali ndi chitchalitchi, iye ali ndi Chikatolika, iye ali ndi Chiprotestanti. Iye wakonza chirichonse, kuti apange chiwonetsero chachikulu.

95 Koma ndine wokondwa kwambiri kuti kuli Atate Kumwamba, Amene ali ndi osewera Ake, nayenso, a sewero lalikulu ili. Pamene wotsutsakhristu awatengera iwo mu imfa iyi ya chirichonse, ngakhale mpaka nthawi ino, Mulungu ndi wokonzeka mu sewero Lake kuti awunyamulire Mpingo Wake kukalowa mu Muyaya, kukalowa mmalo achisangalalo a Muyaya, ndi Mulungu Mwiniwake. Pamene, matupi onyansa akale awa adzasinthidwa ndi kudzapangidwa monga Thupi Lake Lomwe laulemelero, ndipo chivundi ichi

chidzatenga chisavundi, ndipo mu chifanizo Chake ife tidzaima kwanthawizonse.

96 Taonani! Inu amene mumawonera televizioni, inu amene mumamvetsera wailesi, inu amene mumawerenga nyuzipepala zanu, inu amene mumakonda kumva nkhani ndipo mukudabwa kuti ichi ndi chiyani, mvetserani liwu langa: "Mmawa wadza, ndipo usiku ukubweranso." Mmawa ukudza kwa iwo amene akonzekera mmawa, ndipo usiku ukubwera kwa iwo amene sanakonzekere mmawa. Mulungu atakonzekeretsa mitima yathu lero.

97 "Pakuti mmawa udzawala kuwala kwa Muyaya ndi kokongola." Ndipo monga wa ndakatulo anati, "Osankhidwa Ake adzasonkhana ku nyumba zawo kuseri kwa thambo. Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko."

Tiyeni tipemphere.

98 Mu ora ili lolunda pa dziko lapansi, ndi chiwonongeko ku mbali iliyonse, Ambuye Mulungu, ife tiri. . . Ife sitingathe basi kufotokoza momwe tikumverera, ndi kuthokoza ndi kuyamikira mu mtima mwathu, kuti Yesu Khristu anatsika pansi kuchokera ku Ulemelero, ndipo anapangidwa kukhala munthu monga ife, anadzakhala pakati pathu. Ndipo kenako pamene Iye anafera machimo athu, anabwera kudzera njira ya Paradiso, ndipo anadzatenga miyoyo yoyembekezera, anaswa mphamvu iliyonse yauzimu imene mdierekezi anali atamanga nayo dziko lapansi, ndipo anapanga mzere, kuti kuwala kwa dzuwa kwa chisomo Chamuyaya cha Mulungu kuthe kuwalira iwo amene ali ofunitsitsa kulandira iko.

99 Mulungu, perekani lero, kuti anthu kulikonse afulumire, afulumire, adzalowe mu Ufumu, pakuti Uthenga nthawizonse wakhala uli wofulumira. "Fulumirani, fulumirani, tulukani!" Mngelo anati, mu Sodomu, "Sindingachite kalikonse mpaka mutabwera kuno." Ambuye, perekani, kuti ngakhale Uthenga uli wodzaza ndi chisomo, ndi mphamvu, ndi chikondi, komabe ndi wachangu. Perekani, Ambuye, kuti anthu akhoze kubwera mwamsanga ndi kudzamulandira Khristu ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Pakuti Yesu anati, "Iwo amene ali a Mulungu, amamva Mawu a Mulungu." Mulole iwo abwere ndipo adzalape machimo awo, adzabatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu, ku chikhululukiro cha machimo awo, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera; kuti adzakonze moyo wawo mu chikhalidwe chimene mpingo woyamba unali, chomwecho izo zidzakhala pamene Inu mudzabwera.

100 Ndife othokoza chifukwa cha Uthenga, ndipo tikupemphera kuti Inu muwudalitse Iwo, Ambuye, ku ubwino wa mitima yathu, pamene ife tikuyembekezera pa Inu. Mu Dzina la Yesu ife tikupemphera. Ameni.

101 [Malo osajambulidwa pa tepi. Woyimba limba akuyamba kuyimba *Pamene Akuyimba Mabelu Agolide*.—Mkonzi].

Mmodzi ndi mmodzi tidzalowa pakhomo,
Uko kukakhala ndi achisavundi,
Pamene iwo azikaimba mabelu agolide awo kwa inu ndi ine.

102 Kodi inu simukungomukonda Iye? Tsopano, uthenga watha, tiyeni tingomupembedza Iye monga choncho, mu Mzimu. Basi . . . Iye ali pano. Mawu aakulu, amphamvu, koma iwo ndi owona. Ine ndimayankhula izo mu Dzina la Khristu. Kuyandikira kwa tsikulo. Ngati mukunditenga ine . . . Ndikufuna izi . . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

. . . inu ndi ine.

Tiyeni tingokweza dzanja lathu mmwamba.

. . . inu mwamva . . .
Kodi simukumva Angelo akuyimba?
Ndi ulemelero aleluya Chikondwerero.
Mu kukoma kwakutali kumeneko,
Kudutsa mtsinje wonyezimira,
Pamene iwo adzayimba mabelu agolidewo kwa inu . . .

103 Pamene iye akuyimba iyo kenanso, tiyeni tingogwirana chanza ndi winawake pafupi nanu! . . .? . . .

. . . okoma kwanthawizonse,
Kupitirira basi . . .
Pamene a . . . kungofika pa gombe mwa chikhulupiriro . . .

104 Mungonena kwa wina ndi mzake, "Mwendamnjira, ndine wokondwa kwambiri kukhala ndi iwe."

. . . mmodzi tizilowa pakhomo,
Uko kukakhala ndi achisavundi,
Pamene iwo azidzayimba mabelu agolide awo kwa inu ndi ine.

Kodi simukumva mabelu akulira tsopano?
Kodi simukumva Angelo akuyimba? (Ndi chiyani?)
Ndi ulemelero aleluya Chikondwerero.
Mu kukoma kwakutali kumeneko,
Kudutsa mtsinje wonyezimira,
Pamene iwo azidzayimba iwo . . .

105 Zimenezo zangobweretsa chinachake mmalingaliro mwanga. Mkazi wanga, kumbuyo uko, akukumbukira izo bwino. Ndinali ndi mwayi wokayendera tchalitchi chakale cha Pisgah, sukulu ya Baibulo mu California. Ndinali ndi utumiki wa usiku umodzi ndi iwo. Ndiyo yakale, nyumba yamagetsi. Ndi malo abwino bwanji! Ine ndinakomana ndi abusa, M'bale Smith.

Inu mukudziwa, iwo amasindikiza pepala. Iwo amathandizidwa. Iwo samatenga chopereka. Chirichonse chimakhala chaulere. Ndipo iwo akhalapo kwa zaka fifite-chakuti zosamvetseka. Izo zinayambira ndi dokotala amene anali wolumala, anabwera ku California kuti adzalandire chithandizo. Adokotala anati, "Palibe chimene chingachitike kwa inu."

Ine ndikukhulupirira anali malemu Dokotala Price kapena winawake, amene anamupempherera iye, uko mchipinda mmawa wina. Iye sanapeze zotsatira zirizonse, mwachiwonekere, pomwepo. Izo sizikutanthauza kalikonse. Chotero, iye anawuyamba. Iye anati, "Mwanjiraina, imzake, ine ndikukhulupirira, ngakhalebe." Ndipo pamene iye anayamba kuponda phazi lake kuchoka mmphepete, mwendo wake wolumala unadzawongoka. Iye anakhazikitsa Pisgah Home.

106 Usiku wina ine ndinali kumeneko, ndikulalikira. Iwo anali atapanikizana mnyumba yoyankhuliramo yayikulu imeneyo, ndipo mahandirede kuchulukitsa mahandirede atayima ponseponse mmisewu ndi chirichonse, kumene iwo anafika kumbuyo. Ndipo Uthenga utatha, chinachake chinachitika, zinthu ziwiri zimene sindinaziwonepo mmoyo wanga. Iwo sanali gulu chabe la anthu amene amakonda kupanga phokoso lambiri. Iwo si gulu la anthu amene amakhala, ali owuma. Iwo anali anthu odzazidwa ndi Mzimu. Ndipo ine ndinasangalala nacho chiyanjano chopambana chimenecho. Ndipo pamene ife tinali . . .

107 Ndisanapempherere odwala, iwo anayamba kuyimba inayake yokoma monga choncho. Ndipo ine ndinayima, ndipo ndinadabwitsidwa. Ine ndinati, "Pali chinachake chikuchitika apa. Ine sindikumvetsa." Ine ndinamvetseranso, ndipo ndimamva makwaya awiri. Ine ndinati, "Pakuyenera kukhala chinachake cholakwika." Ndipo ndinapukusa mutu wanga. Ndipo, ku makutu anga, kenanso. Ine ndinati, "O Ambuye, mwinamwake ndi kubwerera kwa kuyimbako kuchokera kwa kwaya iyi *apa*." Ine ndikumva ina pamwamba *apa*, pamwamba patali, magebulo aatali kwambiri. Ine ndinati, "Izo zikuyenera kukhala pamwamba apo." Chotero ine ndinayenda kuchoka pa nsanja la atumiki, kupita kuno ku chipinda chakwaya. Izo zinali kumtunda uko.

Ndipo ine—ine ndinati kwa mkazi wanga, ine ndinati, "Kodi iwe ukumva zimenezo, wokondedwa?"

Iye anati, "Icho ndi chiyani?"

"Mlongo Arganbright," ine ndinati, "kodi inu mukumva zimenezo?"

Iye anati, "Inde. Ine ndinazimvapo izo kamodzi, mmoyo wanga."

Ine ndinapita kwa M'bale Arganbright, "Kodi inu mukumva zimenezo?"

"Inde."

108 Aliyense ataweramitsa mitu yawo, akuyimba. "Oh," ine ndinati, "mwinamwake. . .Ine—ine ndikufuna kutsimikiza. Sindikufuna kukhala wokaikira, koma, Ambuye, ngati ndiri mboni Yanu, ngati nditi ndikhale mlonda, ndikuyenera kudziwa chimene ndikunena. Ine ndikuyenera kukhala wotsimikiza za ichi."

109 Monga machiritso Auzimu, ngati sindiri wotsimikiza, ine sindinena kanthu za izo. Ngati ine sindikutsimikiza uku ndi Kudza kwa Ambuye, ine sindinganene kanthu za izo. Ndikuyenera kukhala wotsimikiza.

110 Ine ndinabwerereranso pansanja kenanso. Aliyense ataweramitsa mitu yawo.

111 Ndipo kuyitanira paguwa, anthu ambiri amaika manja awo pa zenera, kubwera kwa Khristu. Ndipo iwo anali akuyimba. Pamene ndinafika kuno, ine ndinati, "Ambuye, izo sizingakhale. Anthu awa akuyimba pansi *apa* anali anthu wamba chabe, koma awa pamwamba *apa* zimamveka ngati anali ochepa. . . Mwinamwake thuu kapena firii sauzande akuyimba, *apa*, koma izo zimawoneka ngati panali mwinamwake handirede sauzande pamwamba *pamenepo*." Ndipo anali amodzi mwa maliwu okoma kwambiri, soprano yokwera kwenikweni, ngati maliwu achikazi. Ine ndinamvetsera, ndipo tsemwe linangoyenderera paliponse pa ine.

112 Ine ndinabwerera mmbuyo kenanso miniti yokha. Ine ndinamvetsera. Ine ndinayenda chokwera, mmwamba. Ndinabwerereranso, chifukwa iwo ankangopitirira kumayimba mu Mzimu. Ine ndinamvetseranso. Ilo silinali liwu *ili*. Ine ndimatha kuwamva iwo pansi *apa*, liwu la mtundu umodzi; ndi ili pamwamba *apa*, liwu la mtundu wina.

113 Chotero pamene msonkhano unatha, ine ndinati kwa abusa, "Abusa, ine ndinamva chinachake chachirendo."

Anati, "Chinali chiyani chimenecho, M'bale Branham?"

114 Ine ndinati, "Ndinamva a—mawu a soprano a akazi, maliwu ophunzitsidwa bwino, okondeka kwambiri omwe ine ndinayamba ndawamvapo mmoyo wanga, pamwamba *apo*."

115 Iye anati, "Izo zakhala zikumveka nthawi zambiri pano, M'bale Branham."

116 Ndinali nditawerenga za amayi okalamba. . .Oh, ine ndaiwala dzina lake tsopano, amene ankakonda kupempherera odwala. Ndipo usiku wina abusa atatseka ulaliki wawo, mayi wamng'onoyo anapita pansi kuti akapempherere odwala. Iye anali ndi ana aang'ono faivi kapena sikisi, ndi iye. Ndipo iye anaima ndipo iye anamvetsera. Ndipo ndi Akazi a Woodworth-Etter, ngati inu nonse munawerengapo bukhu lawo. Ndipo iwo

anamva, iwo anati, "Kwaya ikuyimba pamwamba pa kuyimba mu mpingo."

Maliwuwo atasiya, pansi *apa*, Iwo amayimbabe, mwaona. Ndipo ine ndinaima pamenepo.

117 Ndipo pomwepo, kumbuyo komwe kumbuyo kwa chipindacho . . . Mukuona momwe ziriri mwadongosolo, mwangwiro? Tsopano, ine—ine ndimakhulupirira mu kuyankhula mmalirime. Ine ndimakhulupirira kuti ndi mphatso ya Mulungu, imene imakhala mu mpingo. Ine ndikukhulupirira iyo yakhala ikugwiritsidwa ntchito molakwika monga Malemba ena akhala akugwiritsidwa ntchito molakwika, koma alipo enieni. Inde. Ndipo bambo uyu anadzuka kuseri kwa chipindacho, kumbuyo komwe, ndipo ananena pafupifupi mawu foro kapena faivi mu chinenero china. Osati—osati basi . . . Chinali a—chinenero. Inu mumatha kumva. Aliyense anali chete.

118 Ndipo Chinachake chinasuntha pa ine, ine sindinakhalepo ndi kutanthauzira, mmoyo wanga. Ndipo ine sindinagwiritse ntchito izo pamenepo, chifukwa ine ndinali wamantha. Zinthu zimenezo ndi za Mulungu. Iwe sumayenera kusewera nazo izo.

119 Ndipo Chinachake chinati kwa ine, "Abusa apemphera pemphero lachikhulupiriro." Ine ndinachita kutseka pakamwa panga. Ndipo ndinadikirira. Ndipo apa Iwo anabweranso, funde likubwera, ndipo linati, "Abusa apemphera pemphero la chikhulupiriro."

120 Ine ndinaganiza, "Ambuye, ine ndiribe mphatso yotanthauzira. Yanga ndi kupempherera odwala, chotero ine ndiribe mphatso yotanthauzira." Ndipo ndinatsekanso pakamwa panga ndipo ndinaima njii.

121 Ndipo pomwepo abusa anaimirira ndipo anayamba kupempherera odwala. Oh, Iye ndi Mulungu! Matenda anachiritsidwa, paliponse mchipindamo, paliponse. Ndi chiyani chimenecho? Kutuluka kwa tsiku. Patsalira nthambi yaying'ono. Musadandaule. Mulungu sanakhalepo wopanda mboni.

122 Ndikudalira tsopano kuti chachinsinsi china chachikulu, kwinakwake, mwina osati mu liwu la Angelo, koma chinachake chidzamulola wochimwa aliyense, ngati pangakhale otero mchipinda chino, adzadziwe kuti usikuwo ukunka ukudera dera padziko lapansi, ndi mdima wokhudzika. Koma Kudza kwa Ambuye kuli pafupi, nchiyani chikuchita izo. Ndipo monga mlonda wanu, ine ndingati, "Mmawa ukudza." Khalani okonzeka, nyenyezi zammawa, walani!

123 Ndi angati amene angafune kuti akumbukiridwe mu pemphero lotseka tisanapite? Mungokweza dzanja lanu.

124 Wokondedwa Mulungu, Inu mukuwaona anthuwa pamene iwo akweza manja awo. Ndipo iwo ndi owona mtima mu

izi. Ambiri a iwo amene amafufuza mmanyuzipepala, iwo awafufuza anamateture, mabuku ndi zolemba za zinthu zosiyanasiyana, koma komabe sanapeze yankho. Koma apa ilo labwera, mmawa uno, mu Baibulo. "M'mawa ukubwera, ndipo usiku ukubweranso." Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudalitse munthu aliyense pano, amene anakweza manja ake. Ndipo Inu mukudziwa chimene chiri kuseri kwa dzanja lokwezedwalo. Ndipo, Ambuye, ine ndikukhulupirira kuti pomwe iwo akhala tsopano, kuti Mulungu wopezeka paliponse ndi wokhoza kugawa kwa iwo cholowa chawo cha Mzimu umene iwo akuwufunafuna pa ora lino. Mupereke kwa aliyense, Ambuye. Chifukwa cha Mawu Anu ndi chokhumba chawo, ndi lonjezo Lanu Lauzimu lomwe silingalephere, mulole iwo alandire chimene iwo akwezera manja awo, pamene ine ndikupereka pemphero ili mmalo mwawo. Mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole iwo alandire izo. Ameni.

Mulungu akhale nanu.

125 Tsopano tangotsala ndi kanthawi pang'ono kuti . . . Tsopano ife tipempherera odwala. Ine ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti pali chiyembekezo kwa odwala. "Ndine Ambuye Amene ndimakhululukira mphulupulu zanu zonse, Amene ndimachiritsa matenda anu onse."

126 Ndipo ine, modabwitsa basi momwe izo ziriri, ine ndinasunthidwa kanthawi kapitako, kupita kwa mayi wamng'ono wagona pa machira awa. Ndipo iye ndi—akuzunzidwa ndi matenda a Khansa yammitsempha. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ndi amayi ake akhala apa ndi iye. Ndine wotsimikiza kwenikweni. Inde, uko nkulondola, kuti amayi awa amandiuza ine za mwana wawo, ndipo ine ndimayesera kumulimbikitsa iye.

127 Ndipo kuyitana kokha, aponso, ukatha uthenga uwu. Ndikumverera kuti chipulumutso ndi chinthu choyambirira. Machiritso ndi chachiwiri. Machiritso akhoza kukhala mpaka kumapeto kwa moyo wanu, zaka zambiri. Iwo akhoza kukupatsani inu chisangalalo ndi chimwemwe mukadali pano padziko lapansi, koma izo zidzatha ndi zanu . . . pa imfa yanu. Koma solo imene yapulumutsidwa, imakhala ndi Moyo Wamuyaya. Iyo siingafe, kapena palibe chimene chingatenge izo kuzichotsa kwa inu. Iyo yapita mu Mabukhu a Mulungu, kuti idzaukitsidwe mmasiku otsiriza. Chinthu chachikulu ndi chinthu choyambirira, "Choyamba, Ufumu wa Mulungu ndi chirungamo Chake, zinthu zinazo zidzawonjezeredwa."

128 Ine ndikufuna ndingopereka umboni umodzi wa machiritso a matenda owopsa awa amene mzimayi wamng'ono uyu akudwala. Ndipo panali nthawi yapitayo . . . Iwo akhoza kukhalapo mmawa uno. Ine sindimakhala kuno nthawi zambiri kuti ndidziwe uyu ndi ndani. Ambiri a inu sindikukudziwani. Koma panali

mtsikana wamng'ono kuno ku sukulu yathu ya sekondale. Ndipo iye ankadwala matenda a Khansa yammitsempha awa, ndipo anatengedwera kwa dokotala, za zotupa zazikulu izi zikuphulika pa iye. Ndipo iwo anatenga chidutswa cha chotupacho ndipo anachitumiza icho kutali, kuti akafufuze chimene icho chinali. Ndipo chinabwerera, "Matenda a Khansa yammitsempha osachiritsika."

129 Ndipo mayiyo sankafuna kuti mwanayo adziwe chimene vuto lake linali. Ndipo madokotala anawalangiza amayiwo kuti angomulola iye kuti azingopita ku sukulu, chifukwa anali ndi masiku ochuluka oti akhale moyo. Potsirizira pake iwo anafika pa mtima. Ndipo matenda a Hodgkin ndi khansa, ife tikudziwa zimenezo, mmawonekedwe. Chotero iwo anamutumiza a—mtsikana wamng'onoyo kubwerera ku sukulu, kumusiya iye kuti akafe.

130 Mayiyo anachita mantha. Ndipo anandiyimbira ine pa foni, ndipo anati, "Ndikufuna ndimubweretse iye. Koma ine ndamva, M'bale Branham, kuti mmizere yanu ya pemphero, nthawi zambiri, inu mumatchula matenda pamene inu muli ndi kudzoza kwa Mzimu." Iye anati, "Kodi mungadzakhale wachifundo chotero, ngati Mzimu Woyera ungaulule chirichonse chokhudza mwanayo, kuti musadzanene izo?"

131 "Chabwino," ine ndinati, "Ine sindikuganiza kuti Iye angadzaulule izo, ngati Iye sakufuna kuti izo zidziwike." Ine ndinati, "Ine sindikuganiza choncho. Ndipo ku kachisi wanga yemwe kuno, ine sindimakhala kawirikawiri ndi misonkhano ya mtundu umenewo." Ine ndinati, "Ine ndimangowapempherera odwala."

132 Ndipo dona wamng'onoyo anabwera mu mzere. Ndipo ine ndinawafunsa amake, "Kodi ndinu Mkhristu?"

Iye anati, "Ayi."

Ine ndinati, "Kodi mtsikanayo ndi Mkhristu?"

"Ayi."

133 Ine ndinati, "Iyo ndi njira yoyipa yochokera mdziko." Ndipo ndinati, "Inu simudzamuwonanso iye, ngati angapite mu chikhalidwe chimenecho."

134 Chotero pamene dona wamng'onoyo anabwera mchipinda mmawa umenewo. . .Ndipo nadutsa pafupi ndi malo omwewa amene mtsikana wamng'onoyo anapemphereredwa; chomwechonso atero mtsikana uyu, mu maminiti pang'ono. Ine ndinamufunsa iye. Ndinkamudziwa iye. Ndipo ndinati, "Kodi ndiwe dona wamng'ono waku sekondale kuno?"

Iye anati, "Ndine."

Ine ndinati, "Kodi ukudziwa za matenda ako?"

135 Iye anati, “Madokotala anandiuza kuti akuganiza kuti ndikhala bwino.”

136 “Chabwino,” Ine ndinati, “bwanji ngati supeza bwino? Kodi ndiwe Mkhristu?”

Iye anati, “Ayi, bwana. Ine sindiri.”

Ine ndinati, “Kodi ungakonde utakhala Mkhristu?”

Iye anati, “Ndingatero.”

137 Ndipo ine ndinati, “Kodi ungapereke mtima wako kwa Khristu?” Ndipo iye anati atero. Ndipo amayi ake anathamanga ndipo anati iwo atero, nawonso. Chimene, ine ndinawabatiza iwo onse awiri pomwe pano mu dziwe. Ndinamupempherera mtsikanayo.

138 Ndipo nthawi inapita. Ndipo potsiriza mtsikanayo anayamba kupeza bwino, patapita masiku angapo, iye osadziwa limene linali vuto. Ndipo patapita kanthawi, iwo anamutengeranso iye kokamupima, ndipo samapeza kalikonse ka iyo, nkomwe. Pali a . . .

139 Ine sindimakonda kuyankhula zinthu zazikulu za anthu, koma ndimakonda kunena zoona za anthu. Muli mwamuna mu mzinda muno, amene ndi wodziwika bwino, ndi m’bale wabwino wa Chikhristu, kapena iye sakanakhala dikoni wa mpingo uno . . . Ine ndikutanthauza, trastii wa mpingo. Ndipo iye ali pano tsopano. Ndipo anangodzitengera yekha kuti azimukumbukira mtsikanayo. Panali patapita zaka, patapita zaka ziwiri kapena zitatu, mtsikanayo anali atamaliza sukulu yake ndipo ankayenda ndi mnyamata.

140 Ndipo ine ndinakomana naye iye mu msewu tsiku lina, ndipo iye anali wokondwa kwambiri, ndipo anachitira umboni kwa ulemelero ndi mphamvu ya Yesu Khristu, iwo atatha kumuuza iye chimene chinali. Mtsikanayo anakwatiwa. Ali ndi ana. Ndipo akukhala mosangalala.

141 Ndipo abambo ake amabwera ku malo amalonda a mwamuna uyu, kuti adzamete tsitsi lake. Ndipo Bambo Egan pano, amene a—akhala akusunga nkhaniyo nthawi yonseyi. Ndipo mtsikanayo ali bwino bwino ndipo ali bwino. Ndipo izo zakhala motalika bwanji, M’bale Egan? Zaka zingapo zapitazo, sichoncho izo? [M’bale Egan akuti, “Zaka foro, faivi, sikisi zapitazo.”—Mkonzi]. Ndipo iye ali moyo lero, ku umboni wakuti Mulungu amachiza matenda a Khansa ya mmitsempha.

142 Oh, ndi zabwino kwambiri kudziwa, kuti mu maora a kupsyinjika, kuti timakhala ndi pothawirapo. Pothawirapo pamenepo ndi Khristu.

143 Ine ndikufuna kuti ndinene chifukwa cha . . . kwa inu nonse, chinachake chaching’ono mu msonkhano, chimene chachitika kumene. Ambuye anali wabwino kwambiri poyankha mapemphero anu onse, pamene ine ndinapita

Kumadzulo ku msonkhano posakhalitsapa, masabata angapo apitawo, masabata awiri. Ndipo pamene ife tinali ku Tulsa, pa msonkhano waukulu, ine ndinali ku. . .sindinali woti ndiyankhula, chifukwa. . .Ine ndinkayenera kukhala ndi msonkhano kumeneko. Koma atumiki anali ndi zitsitsimutso zina zikuchitika, chotero ine sindikanatha kukhala ndi msonkhano nthawi imeneyo. Koma ine ndinadzerako, kuti ndikamutenge M'bale Arganbright, kuti ndimutengere iye ku California; mkazi wanga ndi ine, ndi Joseph wamng'ono.

144 Ndipo usiku umenewo, pamene ife tinabwera mochedwa, ine ndinamva kuti Oral Roberts ndi Tommy Osborn anali oti alalikira usiku umenewo. Chotero M'bale Arganbright anaimba mmahotelo mpaka iye anapeza kumene ife tinali, ndipo anati, "Bwerani kuno ku msonkhano." Chotero iye anabwera kumeneko, iye ndi M'bale Sonmore, Amuna Amalonda Achikhristu, wamkulu wa chaputala ku Minneapolis. Iwo— iwo anabwera kudzanditenga ine.

145 Ndipo ine ndinalowa, ndipo iwo anali kale akudya chakudya chamadzulo, mu—mchipinda chovinira cha a Mayo, malo opambana. Anthu amamiliyoni atakhala mmenemo. Ndipo chotero inu mukudziwa momwe ine ndimamverera kuti ndipite ku malo ngati amenewo. Ine sindinkadziwa nkomwe magwiritsidwe ntchito a mipeni ndi mafoloko amene iwo anali nawo pa tebulo. Koma ine ndinalowamo.

146 Ndipo pamene ine ndinalowa mmenemo, Oral Roberts anali akulalikira. Ndipo anali akulalikira za kuchuluka kwa moyo, kuchuluka, ndi kuwauza a Christian Business Men, kuti, "Yesu anagwira nsomba, anaziika izo mmakoka, ndipo anali ndi zochuluka kuposa zimene iwo akanatha—iwo akanatha kugwiritsa ntchito." Ndipo M'bale Roberts ndi woyankhula mwamphamvu, monga inu mukudziwira. Ndipo iye anati, "Pali zambiri za aliyense." Ndipo iye anati, "Tsopano, ine ndikumanga a—kachisi cha kuno, mwinamwake palowa mamillioni a madola." Anati, "Iye akumangidwa ndi nsangalabwi woyera." Ndipo iye anati, "Ine ndamanga pafupifupi theka la njira, ndipo ndalama zandithera." Ndipo anati, "Ndiye ine ndinapita kutsidya kwa msewu tsiku lina, kuti ndikawone iye, ndipo mdierekezi anati, 'Iwe ukudziwa chiyani? Anthu azidutsa ndipo aziti, "Icho ndi chimene Oral Roberts anachita."'"

147 Iye anati, "Kenako ine ndinati kwa mdierekezi, 'Koma iwo akuyenera azidzati, "Oral Roberts anayesetsa."'" Izo nzabwino. Ndipo iye anati, "Ndiye izo zinayikidwa pa mtima pa wa banki, kuno mu mzinda, amene anandibwereka ine zoposera, pafupifupi, madola thuu millioni kuchokera ku banki, kuti ndimalizitsire nyumbayo." Mabanki samachita zimenezo. Inu mukudziwa zimenezo.

148 Ndipo iye anati, "Wamalonda wina ameneyo, waku banki,

wakhala pano tsopano." Iye anati, "Ine sindikufuna kutchula dzina lake, chifukwa iye si ndendende wa anthu a Uthenga wathunthu. Koma," anati, "iye ali pano." Ndipo anati, "Ine—ine sindikuganiza iye amadzinenera nkomwe kuti ndi Mkhristu. Koma," anati, "chinachake chinasuntha mtima wake, ndipo anandipatsa ine ndalama." Anati, "Ngati iye akufuna kuyimirira," anati, "akhoza, koma sindimuchititsa manyazi munthuyo."

149 Munthuyo anaimirira, anati, "Sindikuchita manyazi, Bambo Roberts," ndipo anakhala pansi.

150 Kenako ine ndinalowa mkati, ndipo ndinali nditakhala pansi. Kenako M'bale Roberts, mwamsanga pamene iye anatsiriza, anabwera ndipo anadzagwirana chanza ndi ine, ndipo anandikokera ine mmwamba mmikono yake. Ndipo maminiti pang'ono okha, ndiye, ndithudi, anthu ambiri anabwera, inu mukudziwa, akuyankhula pamene ife tinali tikudyabe, ndipo akufuna misonkhano ndi zina zotero, ndi atumiki.

151 Ndipo kenako Demos Shakarian anaimirira. Iye ndi purezidenti wa gulu la Full Gospel's Business Men. Ndipo iye anaimirira ndipo anati, "Inu mukudziwa, ine ndikungomverera kutsogozedwa kuti M'bale Branham atilalikire ife, usikuuno, uthenga wotsiriza."

152 Chabwino, ine sindinadziwe choti ndinene. Ndipo iye anayamba kunena za amuna amene anakhala muno, anati, "Apa pali *Wakuti-ndi-wakuti*. Ndakumana naye lero." Iwo ankandiuza kuti ali ndi nyumba zathunthu zitatu kapena zinai zamu mzinda wa Miracle Mile. Amamillioni ndi oweta ng'ombe, ndi ena otero, ndipo ine ndikananena chiyani mu msonkhano ngati umenewo?

153 Koma, inu mukudziwa, nthawizonse zimakhala bwino kumvera. Chotero ndinadzuka kuti ndiyankhule bwino momwe ndikanathera. Ndipo pamapeto a utumiki. . .Izo zonse sizimakhala za dongosolo kuitanira kuguwa pa malo ngati amenewo. Koma, inu mukudziwa, ine ndapangapo kuitanira kuguwa pa misonkhano ya maliro. Chotero ine ndinaganiza, "Apa pali mwayi wabwino." Ndipo ine—ine ndinaitanira kuguwa. Ndipo amuna olemera onse amenewo ndi akazi anabwera kwa Ambuye Yesu, ndipo anadzapereka mitima yawo kwa Ambuye.

154 Ine ndinali wodabwa ndi miliyoneya mmodzi, mkazi wa miliyoneya atavala chipewa chaching'ono, chokhala ndi nthenga zokongola pansi mozungulira mmbali, mwinamwake chinamutengera iye madola handirede. Ndipo misozi ikuyenderera mmasaya mwake. Anadzandigwira ine pa dzanja, iye anati, "M'bale Branham, mtima wanga wasunthidwa." Iye

anati, “Ine ndimaganiza kuti ndine Mkhristu, mpaka pano.” Iye anati, “Ndikufuna kutumikira Ambuye.”

Ndipo ine ndinati, “Zikomo.”

155 Ndipo kenako mu maminiti ochepa, Chinachake chinati kwa ine, “Pempherera odwala tsopano.”

156 Ine ndinaganiza, “Oh, ayi. Sindingachite zimenezo. Ndasokoneza kale. . . chipinda chovinira chachikulu ichi. Chotero ngati ndipempherera odwala, iwo aganiza kuti ndine wotengeka kwenikweni.” Chotero ine ndinaganiza, “Ndithudi Ambuye sangakhale akundiuza ine zimenezo. Mwinamwake ndangotopetsedwa chifukwa cha otembenuka awa, chotero ndingozemba ndi kukhala pansi.”

157 Ndipo ine ndinapita pansi pa tebulo la woyankhula, kutsikira mmusi mpaka kumapeto, ndipo ndinakakhala pansi ndi M’bale Jack Moore, tinali titakhala pamenepo, tikuyankhulana. Ndipo ine ndinabwezera msonkhanowo kwa purezidenti, Bambo Shakarian.

158 Kenako pamene iye—iye anaimirira, ndipo iye anati, “Inu mukudziwa chiyani?” Oh, Mulungu akuyenera kuti anamukhudza iye pa phewa. Iye anati, “Ine ndikumverera kutsogozedwa kuti M’bale Branham abwerere ndi kudzapempherera odwala.”

Ine ndinaganiza, “Oh, basi ndendende kulondola.”

159 Ndipo ndinaimirira ndi kuwauza iwo. Ndipo ine ndinati, “Ndinamverera chomwecho. Ndipo ine ndikupemphera kuti Mulungu andikhulululukire ine. Koma zimakhala bwino pamene wina wakhudzidwa, nayenso, inu mukudziwa, zimatipanga ife palimodzi kudziwa kuti ndi kugwira ntchito kwa Mzimu.”

160 Chotero ine ndinati, “Tsopano, machiritso Auzimu sikukhudza mtengo wosema. Iwo si chinthu chongoganizira. Ndi Mulungu yemweyo amene anapulumutsa anthu onsewa pano kanthawi kapitako. Iye ndi Mulungu yemweyo amene amachiza anthu onse amene ali pano, basi mwa chikhulupiriro chophweka kungomukhulupirira Iye.” Ine ndinati, “Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?”

161 Ndipo tsopano ku chinsinsi, kwa mpingo wanga. Monga inu mukudziwira, utumiki wanga ukusintha, ndipo, oh, ndi kusintha kwaulemelero bwanji! Oh! Nonsenu mukukumbukira Mawu amene akhala akulira. Ndipo nthawi zonse izo zikachitika, chinachake chimachitika, pamene ine ndipita kukayankhula pa izo, bwerani—bwerani kwa ine, “Nena kwa phiri ili.” Kodi zakhala bwanji? Chakhala chiri chikhulupiriro. Chirichonse chimakhala mwa chikhulupiriro. Chikhulupiriro si chinthu chimene umachichita. Chikhulupiriro ndi chinachake chimene iwe uli nacho.

162 Ndipo ndinaganiza, "Ngati. . .Ine nthawizonse ndakhala ndikuchita manyazi ndi chikhulupiriro changa, ndi anthu, mwabwino monga Ambuye wakhala aliri."

163 Iye wawonetsera zinthu, wandiuzapo masomphenya. Chirichonse chakhala chiri changwiro. Anthu inu mukudziwa zimenezo. Si munthu payekha. Si munthu. Ndi Mulungu amene amachita zimenezo.

Ndipo chithunzi ichi *apa*, momwe icho chayendera padziko lonse lapansi!

Iwo amene ali ku Germany!

164 Ndipo kuno masabata angapo apitawo, mwinamwake alendo kuno sanachiwonepo icho, iwo anajambula china. Ine ndiri nacho kunyumba. Ndi chithunzi cha Ambuye Yesu atayima pambuyo pamene ine ndinali nditaima. Ndipo manja Ake atatambasula, ndipo malirime a Moto akuwuluka kumachokera mdzanja Lake, pamene ine ndinali kuyankhula pa phunziro, "Nenani kwa phiri ili, 'Suntha,' ndipo usakaikire mu mtima mwako, koma khulupirira." Ndipo ife tiri nacho icho. Ndipo chiri mu Techni-. . .Mitundu ya Kodachrome. Ndipo iwo ali nacho kunyumba tsopano. Ndipo iwo akupanga. . .Icho chafufuzidwa tsopano ndi sayansi, ndi zina zotero, ndi ma labotare. Icho chituluka posachedwapa, china, chomwe chikupanga pafupifupi sikisi za izo tsopano mmalo osiyanasiyana, zimene zajambulidwa.

165 Ichi ndi chopambana mwa zonsezo, sichinawonekepo. Apo pali Zake—ndevu Zake, nkhope Yake, mawonekedwe Ake, manja Ake akulendewera kunja. Ndipo ine ndinali nditaima momwemo monga *chonchi*, ndipo pamene Iye anayika manja Ake, inu simungawone nkomwe malo a ine, monga choncho; mutu wanga, kenako mapazi anga pansi, mutu ndi mapazi basi, ndizo zonse zimene zinatsalira. Mukuona? Ndipo Iye—ndipo Iye waimirira ndi manja Ake atatambasula monga *chonchi*. Ndipo ine ndinatambasula manja anga monga *chonchi*, ndikulalikira, ndikuti, "Nenani kwa phiri ili." Ndipo pafupifupi nthawi imeneyo, chinachake chinachitika. [M'bale Branham akukhwatchitsa zala zake—Mkonzi]. Ndipo iwo anajambula chithunzi cha Icho monga choncho. Ndipo apo Icho chinali, kumbuyoko, chonse cha kalala. Ndipo chachikulu, monga momwe Mulungu amakonzera, dengu lalikulu la kakombo wa calla liri pafupi.

166 Iye ndi Kakombo wa Mchigwa. Ndipo kodi inu mumapeza kuti opiyamu? Kuchokera mu kakombo. Uko nkulondola. Kodi ndi wa chiyani Opiyamu wa Mulungu? Mtendere. Opiyamu amangokupangitsa iwe kuiwala mavuto ako onse. Osuta opiyamu, umo ndi momwe iwo amadziphera okha ndi opiyamu ameneyo. Mulungu ali naye Opiyamu. Ameni. Iye amachepetsa ululu uliwonse, amachiritsa matenda onse, amachotsa nkhawa

iliyonse. Bola ngati ife tikupuma mu Opiyamu Wake, ife timakhala pa mtendere.

167 Ndipo dengu lalikulu la kakombo liri patsogolo pomwe, pamene ine ndimayankhula, pa nsanja.

168 Ndipo ndinapempherera odwala, uko ku Tulsa, ndipo ine ndinangoyenda chotsika ndi kumatuluka. Ndipo pafupifupi maminiti teni atadutsa . . .

169 Sindingafune kutchula dzina la mvangeriyo. Koma mkazi amene anali ndi nyamakazi ya nsana, amene ankagwira ntchito kwa mvangeri uyu, iye anali wolemba nkhani. Ndipo iye ankayenera kulemba monga *chonchi*, chifukwa manja ake ndi mapewa zinali zomangidwa. Iye ankalemba monga *choncho*. Ndipo uyu—mvangeri wamkulu ndi wodziwika uyu uko ku Tulsa, anamulemba iye ntchito mu ntchito yake, kuti amupatse iye chochita.

170 Ndipo iye anayamba kuyenda pansi mu holo. Ndipo mwadzidzidzi manja ake anamasuka, ndipo iye anayamba kulumpha ndi kumakuwa, mpaka iye anakopa chidwi cha aliyense kumtunda uko. Ndipo mkazi wokondedwa ameneyo akudzigwetsa pa maondo ake, ndi kumakweza manja ake ndi kumawomba iwo monga *choncho*. [M'bale Branham akuwomba manja ake—Mkonzi]. Ulemelero wa Mulungu, chifukwa Mulungu anali atamumasula iye, mphindi zochepa chabe pambuyo pa pemphero.

171 Ndipo ine ndinazembera mkati, kuti ndikamvere ndi kuwona zimene iye ankanena. Iye anati, "Ine ndimangoyenda kumusi muholo."

Ndipo ine ndinati, "Chabwino, mayamiko akhale kwa Mulungu."

172 Ndipo ine ndinatembenuka, ndinayamba kuyenda njira inayo. Ndipo ndinamva, kumusi uko, ndinawawona ochimwa onse akuthamanga pamodzi, kuti adzawone chomwe chinali vuto. Ndipo apa panali bambo akutenga bwalo, M'bale Gardner, mwamuna yemweyo amene anandipatsa ine suti iyi.

173 Ambiri a inu mukumudziwa M'bale Gardner. M'bale Gardner, mu Binghamton, New York, wogulitsa waku Oldsmobile wa zaka zitatu zapitazi, anagulitsa magalimoto ochuluka a Oldsmobile kuposa munthu wina aliyense mu United States. Ndipo amawuluka mu ndege yakeyake. Ndipo kupitirira pang'ono chaka chatha . . . Dzina lake ndi George Gardner. Ndipo iye . . .

174 Amayendetsa ndege, yekha, anali yekha, ndipo anagwa, ndi ndege, ndipo anaphulitsa mawondo ake, zidendene zake. Ndipo miyendo yake ndi mapazi ake zinali zitauma, ndipo iye ankayenda monga *chonchi*, woyendetsa ndege wake.

175 Ndipo iye analipo pamene pemphero linapangidwa, ndipo iye anadzisuntha yekha kutuluka mu holo imene munali phwandolo. Ndipo iwo anali atamupezera iye chipinda chapafupi, nayenso, kuti asakhale ndi vuto kuyenda mmbuyo ndi mtsogolo. Ndipo apa panali umboni wake. Iye anapita ku chipinda chake ndipo anakakhala pansi; osati nkomwe kuti anali Mkhristu. Ndipo iye anati, “Mwanjira yina, ine ndikumukhulupirira mnyamata wamng’ono wa mutu wadazi ameneyo amene analalikira kumeneko usikuuno.” Ndipo anati iye anayamba kuzindikira zala zake zikuyamba kugwedezeka. Ndipo analumpha pa mapazi ake, chirichonse kulunga.

176 Ataimirira kunja uko, akumulemekeza Mulungu, ataimirira, akukweza miyendo yake mmwamba-ndi-pansi monga *choncho*, ndi mmbali mwa mapazi ake ndi chirichonse, akungochitira umboni kwa ulemelero wa Mulungu.

177 Kamodzinso, ife tisanapempherere odwala. Ine ndinkakhala ndi M’bale Arganbright. Ndipo mzanga wabwino, Leo ndi Gene, amadziwa chimene kuyimba kwa mafoni kuli. Foni ikayitana, ndipo M’bale Arganbright amayankha. Ndipo, inu mukudziwa, sungakhale konsekonse. Koma, zinachitika kuti, kuti ine ndinayankha foniyo.

178 Ine ndikukhulupirira kuti zonse zimagwira ntchito mu njira yoperekedwa ya Mulungu. Kodi inu simukukhulupirira? Ndikukhulupirira ndi chifukwa chake dona wamng’onoyo ali pano. Ndikukhulupirira kuti ndi chifukwa inu nonse muli pano. Ine ndikukhulupirira ndi chifukwa chake ine ndiri pano, kuti ife takumana pamodzi kwa ulemelero wa Mulungu, pa chifukwa china. Nchifukwa chiyani ife tabwera kudutsa malo achisanu, kuti tidzakhale pano mmawa uno?

179 Chotero ine ndinatenga foni, chifukwa M’bale Arganbright sanali mchipindamo. Ndipo anati, “Ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa M’bale Branham.”

Ine ndinati, “Ine ndine M’bale Branham.”

180 Iye anali bambo wa Chispanishi. Iye anati, “Bwana, ndikudziwa kuti izo sizomveka, pafupifupi, kuti ine ndifunse funso limene ndikufuna ndifunseli.” Iye anati, “Ine ndikhoza kulingalira momwe anthu amakokera, ndi zina zotero. Koma,” anati, “Ndine mmishonare ku Mexico.” Ndipo anati, “Kumbuyo kuno, ndimakhala kuno ku La Crescenta. Ndipo ine ndangomva, maora pang’ono apitawo, kuti inu munali mu mzindamu.” Ndipo anati, “Ine ndamubweretsa mwana wanga, kuti ndidzayesere kumubweretsa iye kwa inu kapena M’bale Roberts, kapena ena a abale amene amapempherera odwala.” Ndipo iye anati, “Pokhala kuti ndi mwana wanga, chikhulupiriro changa, ine ndikuganiza, changokhala chofooka pang’ono.” Iye anati, “Mwana wanga sanakwanitse miyezi foro ndipo akufa ndi khansa.”

Ndipo Chinachake chinati kwa ine, "Pita kwa mwana ameneyo."

181 "Chabwino," ine ndinati, "bwana, ine ndimutenga M'bale Arganbright, ndipo inu mumuuze iye kumene mwanayo ali, ine ndikakumana nanu." Chotero iye anatenga . . . Ine ndinamutenga M'bale Arganbright, ndipo amamuuza iye.

182 Chotero ife tinalowa mgalimoto ndipo tinapita kumusi uko. Ndipo ndinakumana ndi mkazi wake wamng'ono. Ndipo iye pokhala waku Mexico, ngakhale sankawoneka chomwecho. Anali wa khungu loyera, labwino, koma anali wa ku Mexico. Chimene, aku Mexico, nthawi zambiri, amakhala a mzindo, chifukwa iwo amabwera pakati pa Achispanishi ndi Amwenye. Ndipo pamakhala ena a Amwenye awo amene amakhala ndi mzindo, oyera ngati chipale. Ndipo kenako mkazi wake anali wachi Finnishi, mosamalitsa wa mzindo, mkazi wamng'ono wokoma kwambiri.

183 Ndipo ine ndinapita ku chipatala ndi iye, kuti ndikamuwone mwana wake. Nditalowa mchipindacho, iwo anali naye pafupi ndi likulu la anamwino. Pakuti, mwana wamng'onoyo, komabe wa usinkhu wa miyezi foro yakubadwa, anabadwa ndi zotupa zazikulu mu nsagwada, zimene zinatupa pafupifupi kutalika *chomwecho* ndi nkhope yake, monga *choncho*, basi zitatuluka monga choncho. Ndipo madotolo anali atayesera kuti apange opareshoni. Ndipo zipsyera zazikulu zakuya zinali zitadula mozungulira pakhosi pake, njira yonse mozungulira. Izo sizinaimitse izo; kokha izo zinathamangira mu lirime lake. Ndipo nsagwada zazing'ono zikulendewera monga *choncho*, ndi zipsyera zazikulu zakuya. Ndipo lirime lake laling'ono . . . Kamwa yaing'ono osati yaikulu *motero*. Ndipo lirime lake, mwinamwake lalikulu *choncho*, litatupa, linali litakankhidwira kunja kutali *chomwecho*, ndipo litasanduka lakuda. Ndipo linatseka kupuma kwa mphuno kumatsikira mmusi, pamene ilo linatupa mmwamba mwa kamwa lake. Ndipo ndithudi, ilo linadula mpweya wake, kuchokera *apa*. Iwo ankayenera kuboola bowo pakhosi pake. Ndipo anali ndi wiziro yaying'ono ya pang'ono . . . ngati chitini chaching'ono mozungulira pakhosi pake. Ndipo mikono yake yaing'ono inali yomangirira, monga *chonchi*, kuti iye asamakhoze kufikira kukakoka wiziro imeneyo; iye angatsamwidwe. Ndipo khansa, ikuwukha, ndipo namwino amachita kuyima pamenepo ndi chinachake choti chizikoka chinyezi cha khansayo kuchokera mu wiziroyo, kapena izo zingamutsamwitse nkufa.

184 Ndipo abambowo anayenda mozungulira kupita pa bedi, ndipo iwo anati, "Ricky, mnyamata wamng'ono wa adadi!" Iye anati, "Adadi amubweretsa M'bale Branham kuti adzakupempherere iwe, Ricky."

185 Pamene iye anati, "Mnyamata wamng'ono wa adadi," mzimu

wanga unangondisiya ine. Ine sindikanazipirira izo motalika. Ine ndinangogwira mmbali mwa bedi. "Mnyamata wamng'ono wa adadi." Ndipo mwana wamng'onoyo, komabe wachinyamata monga iye anali, ankadziwa kuti awo anali adadi ake. Ndipo iye anayamba kupuma monga choncho, ndi mikono yake yaing'ono monga choncho. Ndipo iye akuyesera kuti amusisite mwana wamng'onoyo pa mutu. Mwana wamng'ono wosauka, wobadwa mu chikhalidwe chimenecho. Ine sindinathe basi kuti ndiyankhule. Ine basi. . .Inu mukudziwa, iwe umangokhala wokhuta kwambiri, iwe sungakhoze kunena chirichonse.

186 Ine ndinayang'ana pansi, ndinawona manja aang'ono kwambiri amenewo atatuluka pansi pa zingwe zazikuluzo. [M'bale Branham akupanga phokoso lopuma—Mkonzi]. Ndipo akupanga phokoso lopuma. Ndipo ine ndinaganiza, "Kodi zimenezo si zomvetsa chisoni!"

187 Ndipo nditakhala ngati ndabwerera kwa ine mwini, mokwanira kuti ndiganize chinachake, Ine ndinaganiza, "Yesu, kodi mukutanthauza kuti Inu mumasangalala mukamawona zimenezo? Ine sindingakhulupirire izo. Ine sindingakhulupirire basi kuti Inu mumapeza ulemelero kuchokera mwa mwana wamng'onoyo akuzunzika monga choncho. Izo sizingatheke. Ngati izo zimandipangitsa ine, wochimwa, kumverera momwe ine ndikuchitira kwa mwana ameneyo, kodi izo zingachite chiyani kwa Inu, gwero la chifundo chonse? Kodi izo zikuyenera kuchita chiyani kwa Inu?" Ndipo ndinali ndisananenebe mawu.

188 Iye ankayesera kuti asewere naye iye, kuti amutontholetse iye chete. Ndipo thupi lake laling'ono litavala thewera laling'ono, basi pafupifupi. . .Thupi laling'onolo, ndi zonse, osati kupitirira kukula *chomwecho*. Ndipo mutu wake unali gawo lalikulu kwambiri, nsagwada yake itatupa kwambiri. Ndipo iwo anali ndi chinachake mozungulira mutu wake, kuwopetsa kuti mutu wake waung'ono usaphulike. Inu mukudziwa, nsanza; nsagwada zake zinali zitatupa kwambiri, zitatuluka monga *choncho*, kuti zisaphulike. Ndipo namwinoyo anali ataima pamenepo.

189 Ndipo ine ndinayang'ana pansi kwa mwanayo, ndipo ine ndinaganiza, "Ambuye, Inu mukanachita chiyani ngati Inu mukanaima pano?"

190 Tsopano, ine ndikuzindikira kuti ine ndiri pa guwa. Ndipo ine ndikuzindikira kuti Mulungu ali pano. Koma zinkawoneka kwa ine kuti Chinachake chinayankhula pansi mmoyo wanga, ndipo chinati, "Ndikuyembekezera kuwona chimene iwe utachite za izo. Ine ndinapereka ulamuliro Wanga kwa Mpingo." Pamenepo iwe wabwereranso kuti, "Udzanene kwa phiri ili." "Ine ndinapereka ulamuliro Wanga kwa Mpingo, ndipo Ine ndikuyembekezera kuwona chimene iwe uti uchite."

191 Ine ndikudabwa ngati awo ali machitidwe Ake kwa ife tonse nthawi zonse, kuti Iye akuyembekezera kuti awone chimene titi tichite. Nanga bwanji zizindikiro za nthawi imene takhala tikuilalikira? Kodi Iye akanadzachita chiyani? Iye akuyembekezera kuti awone chimene tingachite.

192 Chabwino, ine ndinayika dzanja la mwana wakeyo mu langa, mu zala zanga basi, monga *choncho*. Ilo linali laling'ono kwambiri. Ndipo ndinati, "Ambuye, imvani pemphero la wantchito Wanu. Ndipo mwa chikhulupiriro, kuti ine ndikukhulupirira kuti Inu muli, ine ndikuyika pakati pa chiwanda cha khansa ichi ndi moyo wa mwanayu, Magazi a Yesu Khristu. Pakati pa wokupha ndi mwanayu, Magazi, mwa chikhulupiriro ine ndikuyika izo." Ndipo sindinathe kunena china chirichonse.

193 Ine ndinangotembenuka ndi kuyamba kutuluka. Abambowo ananditsatira ine. Iye anati, "M'bale Branham, Ambuye akuyika pa mtima wanga kuti ndikupatseni inu zakhumi zina."

194 "Oh," Ine ndinati, "m'bale, musaganize za zimenezo. Ayi." Ine ndinati, "Sindikufuna ndalama, m'bale."

195 Iye anati, "Koma ndinasungira chakhumi." Oh, ndalama pang'ono, ine ndaiwala tsopano ndendende basi, ine ndikukhulupirira pafupifupi madolla fifite. Iye anati, "Ambuye anachiyika icho pa mtima wanga kuti ndipereke icho kwa inu."

196 Ine ndinati, "Ine ndikuuzani inu chiyani. Ine ndilandira icho, ndipo kenako inu mutembenuke ndi kuchipereka icho kwa Ricky wamng'ono apo, pa yake—pa bilu yake ya kuchipatala. Chifukwa, ndinu mlaliki. Ine ndikudziwa chimene izo ziri, chimene ndalama zimatanthauza. Ndipo inu, mmishonare, ndipo ine ndikudziwa kuti zimatengera ndalama. Ndipo inu muli ndi banja, ndi mabilu onse a adokotala awa. Kaziyikeninso izo pa bilu ya Ricky wamng'onoyo."

197 Iye anati, "Ine sindikufuna kuti ndichite zimenezo, M'bale Branham. Izo si zolipirira madokotala. Izo ndi zolipira atumiki."

198 Ndipo ine ndinati, "Inde, koma ine ndikubwezera izo kwa inu." Ndipo ine ndinazikana izo.

199 Ndipo ine ndinapitirira kupita ku nyumba, ndipo mu maora pang'ono, nsagwadazo zinaphwera, ndipo lirime lake linabwerera mmalo ake. Mulungu anamuchiritsa mnyamata wamng'onoyo. Iwo ankachotsa wiziro mmawa umene ine ndinachoka, kukhosi kwake.

200 Icho chinadodometsa Gombe lonse la Kumadzulo. Dokotala wotchuka anatumiza mwana wake wamwamuna, ndi mdzukulu wake. Ndipo iwo anadula msewu, kutali, mailosi forte kapena fifite uko, mu Pasadena, ndipo anadula msewu kumene ine ndimati ndidutse, kuti ndikamupempherere mwana amene anali ndi kusokonekera mu ubongo. Iwo anali atamupatsa

iye peniselini, ndipo anapangitsa khansa kubwera kuchokera ku zotsatira za peniseliniyo mchiuno mwake. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti Ambuye anamuchiza iye.

201 Tisanatuluke mnyumbamo, foni inalira, inkangolira. M'bale Arganbright, ine ndinamumva iye akukangana ndi winawake, anati, "Ayi, sindingachite zimenezo."

202 Basi pamene ndinkakwera mu galimoto, panali a—galimoto yaing'ono imene inabwera. Kodi anali ndani koma m'bale wanga wamng'ono waku Mexico ndi mkazi wake! Awiri onsewo akungolira ndi kumatamanda Mulungu. Anati, "M'bale Branham, ine ndabweretsa zakhumi izi kwa inu."

203 "Oh," ine ndinati, "m'bale, ine sindingalandire izo." Ine ndinati, "Ine basi sindingachite zimenezo."

Iye anati, "Koma ine ndabweretsa izo kwa inu."

Anati, ine ndinati, "Ndinakuuzani inu kuti muziyike izo pa bilu ya Ricky."

204 Iye anati, "Mmawa uno, pamene ine ndinapita kukamupatsa dokotala zakhumi izi, kuti zipite pa bilu ya Ricky, dokotalayo anati, 'Iwe ulibe ngongole ndi ine.' Iye anati, 'Ndinalibe chochita ndi izo.' Iye anati, 'Chimenecho ndi chozizwitsa chachikulu.' Iye anati, 'Ine. . .Iwe ulibe khobidi limodzi la ine.'" Chotero iye anati, "Tengani izi, M'bale Branham. Ambuye anandiuza ine kuti inu mukuyenera kutenga izo."

205 Ine ndinaganiza, "Oh, sindingathe." Ine ndinati, "Ambuye, sindikumverera kuti ndichite zimenezo."

206 Kenako chinachake chinabwera kwa ine. Yesu atayima tsiku lina, akuyang'ana olemera akuponya ndalama zawo zochuluka. Oh, iwo anali ndi zochuluka, chotero iwo anali akupereka zochuluka. Ndipo mkazi wamasiye wamng'ono anabwera ndi makobiri atatu, ndipo izo zinali zonse zimene iye anali nazo. Ndizo zonse zokhalira moyo zimene iye anali nazo, ndipo iye anaziponyera izo mkati. Tsopano kodi ife tikanachita chiyani? "Oh, mlongo, musachite zimenezo. Huh-uh. Inu mukudziwa, ife sitikuzisowa izo. Musaponye izo mmenemo. Ndizo zonse zokhalira moyo zanu." Koma Yesu anangomulola iye kuti apitirire ndi kuchita izo, pakuti, "Ndi kodalitsika kupereka kuposa kulandira."

207 Ine ndinalandira zakhumi zazing'onozo. Ine sindinadziwe zochita nazo izo. Ine ndikaziika izo kwinakwake, mu ntchito ina kwa ulemelero wa Mulungu, kwinakwake mopambana momwe ine ndingathere.

208 Izo ndi chiyani? Ndi Ulemelero wa Mulungu. Ndi Mphamvu ya Mulungu. Mithunzi ikugwa; Khristu akuwonekera, ndi chifukwa chake zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwonekera. Ndi Kuwala kwa Mwana kwakukulu kuja kukunyezimira kuchokera mu nyenyezi za mmawa, ndi machiritso mu mapiko

Ake. Ndipo ngati Iye angabweretse machiritso kuchokera mu chinyezimiritso cha Kukhalapo Kwake, kodi Iye adzachita chiyani pamene Iye adzabwera mwa Munthu? Matupi achivundi athu awa adzasinthidwa ndi kupangidwa mofanana ndi Thupi Lake Lomwe la ulemelero. Kodi izo zidzakhala chiyani pamene Iye adzabwera? Mpaka Iye adzabwere, ife ndi othokoza chifukwa cha Kuwala kwa Mwana wa Kukhalapo Kwake, monga nyenyezi za mmawa zimakwera zotchinga za Ulemelero, ndi kukhala pamenepo kuti zizitamanda Kudza Kwake mu ora la mdima ili.

Tiyeni tipemphere.

209 O Ambuye, ife timangokukondani Inu mochuluka kwambiri mpaka, Ambuye, palibe kunena motalika bwanji. . . Ife sitimatopa kuchitira umboni za matamando Anu. Koma ora lafika tsopano, pali anthu odwala akuyembekezera. Inu mukudziwa maumboni awa. Iwo ali, monga momwe ine ndikudziwira, Ambuye, choonadi chenicheni. Za woyendetsa ndege atayima kunja uko, akuwonetsa momwe iye angaimire pa mapazi ake, ndi zochitika zonse zimene thupi lake linali; ndipo anakokera mmwamba miyendo ya buluku lake ndi kuwonetsa mawondo ake ndi miyendo yonse yophulika ndi ya zipsyera, pamene madokotala anayesera kubwezeretsa mafupa pamodzi. Inu munamuwona mkazi atayima pamenepo ndi penti pa nkhope yake, ndipo iyo ikutsukika ndi misonzi ya chisangalalo, pamene iye anauzidwa za matenda ake a nyamakazi anali atachiritsidwa ndi Mphamvu Yanu. Ndi za mwana wamng'ono wokondedwa uja, ndi umboni wa abambo ndi iwo amene analipo.

210 Tsopano, Ambuye, Inu ndi wamkulu basi pano mmawa uno, muno mu kachisi, monga Inu muliri kulikonse mdziko. Ndipo Inu munalonjeza kuti pamene ife tidzakomana pamodzi, kuti Inu mudzakhala pakati pathu. Tsopano ife tiyitanira odwala amene Inu mwawatumiza kwa ife mmawa uno. Ndipo ife tiwapempherera iwo, ndipo tipemphera ndi mitima yathu yonse, pemphero la chikhulupiriro. Ndipo Inu mupulumutse odwala ndipo muwadzutse iwo. Ndipo ngati iwo anachimwa, akhululukireni iwo, Atate, pamene ife tikuvomereza zolakwa zathu wina ndi mzake, ndi kupempehererana wina ndi mzake. Ndipo Inu munati, "Pemphero lochita, mwamphamvu la munthu wolungama limachita kwakukulu."

211 Ife tikudziwa za mmodzi wagona pano ndi ife mmawa uno, mayi wamng'ono chabe ali ndi ana aang'ono awa. Ambuye, malingana ndi madokotala, iye ali pafupi ndi mapeto a ulendo wake. Koma ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu muyime pakati pa iye ndi mdani ameneyo. Ndipo pamene ife timudzoza iye ndi kumupempherera iye, mulole Mphamvu Yanu ikhudze moyo wake umenewo. Izo zibweretse chikhulupiriro ndi chiwombolo. Ndipo mulole iye apite kwawo ndipo akakhale bwino, ndi kupereka matamando, ndipo

akakhale a—chinyezimiritso cha Nyenyezi ya Mmawa, kwa ulemelero wa Mulungu. Ameni.

212 M'bale Mercier, tsopano, pamene ife tikuwatenga anthu awa mmene zakonzedwera, anthu akubwera. Ife tingoyitana nambala iyi. Ndipo iwo ayikidwa pa mndandanda wa iwo oti apemphereredwe.

58-1130 Mlonda, Ndi Nthawi Yanji Ya Usiku?
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org